


# *KUMVA, KUZINDIKIRA,*

## *NKUCHITAPO PA*

### *MAWU A MULUNGU*

 Tsopano, matepi awa, a msonkhano uwu mmawa uno, sakugulitsidwa, iwo ndi a Mpingo basi kapena a winawake, chifukwa iwo ndi a Chiphunzitso. Ndipo mmisonkhano kunja uko, izo zimayambitsa chisokonezo, chifukwa pafupifupi awiri a ife sitimawonana mwangwiro diso kwa diso, koma ife tikuyenera kukhala mtima kwa mtima, mulimonse. Koma izo, ife mu kachisi kuno, matepi awa ali, inu muzindikira pa... Ndi a abwenzi okha, ndi zina zotero.

<sup>2</sup> Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe ku pemphero. Ndi angati amene angafune kuti akumbukiridwe pamene mwaweramitsa mitu yanu? Basi pokweza dzanja mmwamba, kunena, “Ambuye, ndine—ndine wosowa lero, ndipo ndikusowa chisomo Chanu,” chirichonse chimene icho chiri.

<sup>3</sup> Atate athu Akumwamba, ife tsopano tikuyandikira Mpandowachifumu Wanu wachifundo, chifukwa ife tafunsidwa kuti tichite izi. Ndipo izo zinanenedwa kwa ife ndi Mwana Wanu, ndi Mpulumutsi wathu, kuti ngati ife tingakupempheni Inu chirichonse mu Dzina Lake, icho chidzaperekedwa. Chotero, Ambuye, podziwa kuti ife tikukhala mu mithunzi ya Kudza Kwake, ndipo tsopano tayima mu mithunzi ya chifundo Chake, ndiye ife tikupempha, Ambuye, kuti Inu musankhe, mwa Mzimu Woyera, zinthu izo zimene ife tikuyenera kuzipempha. Ndipo ife tikumverera mmawa uno, kuti izo sizikanakhala zosiyana ndi Mawu Anu kapena kwa chiyeo Chanu chachikulu, ndi chifundo Chanu ndi chisomo, kuti ngati ife tikanati tipemphe kuti ife tikhale ndi kuyenderedwa kwapadera lero kuchokera kwa Mzimu Woyera. Kuti Iye akhoze kubwera pakati pathu ndi kudzazindikira maganizo a mmitima yathu, kuulula kwa ife malo athu ofooka, ndi kuchiza matenda athu, ndi kumanga mitima yosweka, ndi kupulumutsa otayika, ndi kukonzekeretsa anthu pa Kudza Kwake. Ambuye, imvani pemphero ili.

<sup>4</sup> Tsopano ife tiwerenga Mawu Anu. Ndipo—ndipo ife tikupemphera, Ambuye, kuti pa phunziro lathu la Sande sukulu mmawa uno, kuti Inu mubweretse gawo lowerenga ndipo muulule Izo ku mitima yathu. Chifukwa, ife timabwera kuno ndi cholinga chimodzi. Cholinga chimenecho, chokha, ndi kuti tikudziweni Inu bwinoko. Ife amene tiri Akhristu,

mwa Chikhulupiriro, tikufuna tikudziweni Inu bwinoko. Iwo amene sanakhale Akhristu, akufuna kuti akudziweni Inu monga Mpulumutsi wawo. Iwo amene akudwala akufuna kuti akudziweni Inu ngati Mchiritsi wawo. Ndipo ife tikupemphera kuti pasakhale mmodzi wochoka mnyumba muno, wopanda kanthu, koma kuti pempho lirilonse likwaniritsidwe mwathunthu, ndipo chokhumba chirichonse chikachitike, ndi aliyense—munthu aliyense akhale wokondwa, ndipo achoke mnyumbayi, akunena, monga aja ankachokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siinantenthe mkati mwathu, pamene Iye amayankhula nafe pa njira?” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>5</sup> Tsopano kwa inu amene mukufuna kutsegula Bukhu lanu. Kawirikawiri, ine ndapezapo, kuti mu mautumiki a uvangeri, kuti pafupifupi maminiti twente kapena sarte okha amakhala ndi chochita chopambana kwa uthenga wauzimu woonyera mkati, ndipo kenako kuyitanira kuguwa. Koma iyi pokhala Sande sukulu, ine sindikufuna basi kuti ndichite izo mwanjira imeneyo mmawa uno. Ine ndikumverera kutsogozedwa kwambiri kuti nditenge nthawi yanga ndi kuyankhula pa Mawu.

<sup>6</sup> Tsopano, ngati aliyense sakumasuka, kwazizira kwambiri, chinthu chokhacho chomwe mukuyenera kuchita ndi . . . M’bale wanga, woyang’anira, ali kuseri kwa tchalitchi kumeneko, ingokwezani mmwamba dzanja lanu monga *choncho* kumbuyo uko, kwa iye, ndipo iye asintha kutenthako. Ndipo ife tikufuna kuti mukhazikike komanso kuti muzimverera bwino. Ndi kumamvetsera ku Mawu, pakuti ife tikudalira Mzimu Woyera kuti utiphunzitsa ife Mawu a Mulungu. Ndipo kodi inu nonse mukumva bwino, kumbuyoko? Ngati mukukwanitsa, kwezani manja anu, ngati inu—mukumva bwino bwino. Izo nzabwino.

<sup>7</sup> Tsopano ndikufuna kuti inu mutsegule ndi ine, ine ndiri ndi mitu ina yomwe ndalemba apa, ndi Malemba ena. Chotero ine ndikufuna kuti inu mutembenezire ndi ine, choyamba, ku Bukhu la Aroma, Aroma, mutu wa 9. Ndipo ife tikufuna kuti tiwerenge kwa phunziro la Malemba, choyamba, mu Aroma 9:11.

*(Pakuti anawo asanabadwe, asanachite chabwino kapena choipa, kuti cholinga cha Mulungu monga mwa kusankhidwa chikhale, osati cha ntchito, koma cha iye amene amayitana;)*

*Zinanenedwa kwa iye, Wamkulu adzatumikira wamng’ono.*

*Monga kunalembedwa, Yakobo ine ndamukonda, ndipo Esau ndinamuda.*

<sup>8</sup> Mulungu awonjezere madalitso Ake pa kuwerenga kwa Malemba uku. Ndipo tsopano kwa mutu, kuti ndichirikize phunziro langa, ine ndikufuna kuti nditenge uwu ngati mutu:

*Kumva, Kuzindikira, Nkuchitapo Pa Mawu A Mulungu.* Ndiroleni ine ndibwereze izo kachiwiri. “Kumva, ndi kuzindikira, ndipo kenako nkuchitapo pa Mawu a Mulungu.”

<sup>9</sup> Tsopano, ife tikudziwa bwino, ife anthu amene timafufuza Malemba usana ndi usiku, ndi kuwerenga mapepala athu ndi kumva owerenga nkhani, kuti dziko ili tsopano likuima mu mphamvu ziwiri zazikulu zauzimu. Ndipo ziwiri zonsezo ndi mphamvu zachipembedzo. Ndipo ndikukhulupirira kuti mphamvu zazikuluzi posachedwapa zidzafika ku mutu. Ndipo ziwiri zonse za mphamvu zazikulu izi zinaimiriridwa mwa ana awiri awa a Isaki. Momwe kuti Mulungu, mu nzeru Zake zopanda malire, waphimbiratu zinthu zonse kwa ife; kuti ife tikakhoze mwa zinthu izi kudziwa, za chinachake, chimene chiri patsogolo pathu. Anazipanga izo momveka bwino, kuti Mulungu ndi Mawu Ake, ndi chirengedwe ndi miyamba Yake, zinakonzedwa mwangwiwo kwambiri pamodzi, kuti ngakhale—wochimwa akhoza kuwona chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Mulungu anazikonza izo. Palibe amene alibe chowiringula.

<sup>10</sup> Tsopano, ife tikuwona mwa ana awiri awa kuti pamene iwo, iwo asanabadwe nkomwe, iwo anali pa nkondo wina ndi mzake. Ngakhale kuti amayi awo namwali. . . Pakuti, iye anali namwali, Rebeka wokongola amene anakwatiwa ndi mbewu yolungama ya lonjezo la Mulungu, Isaki; kuti iwo anali awiri opatulika, okhulupirira odzazidwa ndi Mzimu pa Mulungu, anazozedweratu ku ukwati omwewo umene iwo analumikizana nawo. Mulungu anadziwiratu izo. Ndipo chinthu choterocho chikanakhoza bwanji kubwera kudzera mwa mayi mmodzi ameneyo, mwa bambo mmodzi? Mmodzi, munthu woyipa kwambiri; ndipo wina, munthu wabwino kwambiri; ndi momwe kuti munthu wabwino ankawoneka ngati woyipa, ndi woyipa ankawoneka ngati anali wabwino.

<sup>11</sup> Tsopano izo ziri, nthawizonse zakhala ziri, nthawizonse zidzakhala dongosolo la Mulungu. Mulungu sangasinthe dongosolo Lake. Chifukwa, Iye amapanga dongosolo Lake mwangwiwo, chifukwa ndi gawo la Iye.

<sup>12</sup> Mmunda wa Edeni, tchimo linali lokongola kwambiri mpaka linamukopa Eva kuchoka ku chirungamo, kupita ku tchimo. Ndipo mmunda momwemo mmene munali mtengo wa Moyo, munalinso mtengo wa imfa.

<sup>13</sup> Ife tingawudziwe iwo lero ngati lamulo la kutsutsana. Kutu, pamene pali chabwino, pali choyipa; pamene pali cholondola, pali cholakwika. Ndipo ife sitidzatha, mosasamala momwe zotizungulira zingakhalire, kudzigwedeza tokha pamaso pa ziwirizi. Chifukwa, Paulo anati, “Ndikafuna kuchita chabwino, choyipa chimakhala pomwepo.” Wochimwayo sadzatha konse kudzigwedeza kuchoka kwa Mkristu, Mkristu kwa

wochimwayo. Padzakhala mboni pamenepo ya chabwino, ndi umboni wa cholakwika, nthawizonse. Ndipo inu mumapanga kusankha kwanu. Inu mukuyenera kutenga mbali imodzi kapena imzakeyo.

<sup>14</sup> Koma mwa ana awiri awa, nzodabwitsa kudziwa kuti, iwo asanabadwe, awiri onsewo mbewu yofanana, yochokera kwa Isaki, imene inali lonjezo. Tsopano, phunziro lathu ndi lalitali pang'ono, ndipo ine ndikufuna kukhala ndi maziko okwanira mpaka inu muthe kuwona ndendende chimene ine ndikukamba. Ndipo mwana woyamba, Esau, amene anabadwa; ife tikupeza kuti iwo sankangokangana kokha ndi kumenyana mmimba mwa mayi wawo, koma iwo anatuluka kwa iye, akumenyana, Esau akubadwa, ndipo Yakobo atagwira chidene chake. Ndipo iwo akumenyanabe.

<sup>15</sup> Ndipo momwe izo, momwe izo zikanakhoza kubwera kuchokera kwa bambo kapena mayi wangwiro, woyera, wosankhidwa, woyera, wopatulidwa ameneyo! Chotero kuti tikhazikitse izo, kuti, Mulungu amaitana mwa kusankha. Izo zikuyenera kukhala. Ziribe kanthu momwe abambo anu ndi amayi anu anali abwino, momwe iwo anali abwino, momwe abambo anu ndi amayi anu anali Akhristu, izo zimakhallabe kwa inu monga munthu payekha, mayimidwe anu pamaso pa Mulungu. Phunziro ili likuphunzitsa zimenezo, kuti iwo, ana awiri onsewo, analipo ngakhale mwa osankhidwa ndi oitanidwa a Mulungu, abambo ndi amayi, mkazi namwali ndi mwamuna woyera, amene potsirizira pake anadzatsika kudzakhala ngakhale kudzera mu mbewu yake anadzabwera Yesu Khristu. Iye anabadwa monga mmodzi wochokera kwa akufa. Iye anayesedwa, atate ake pambuyo pa iye. Ndipo iye analonjezedwa, kupyolera mwa mbewu iyi ya Isaki, kuti dziko lonse lidzapulumutsidwa. Ndipo kuchokera mwa munthu ngati ameneyo, ndipo magazi ake angwiro kwambiri mwakuti Mulungu sakanamulola ngakhale Mfilisti kuti amukhudze mayiyo, Abrahamu atamupereka iye kwa iye. Mulungu anakantha nyumba yake, ndipo anati, “Iwe ndi chimodzimodzi ngati wakufa,” akuwugwira mtsinje wa magazi umenewo kuti ukhale wangwiro. Ndipo Rebeka ameneyo, mayi wolungama, woyera, wotumizidwa ndi Mulungu ndi woitanidwa ndi Mulungu. Ndipo kuchokera ku mbewu yopatulika imeneyo kunadzatuluka chigawenga ndi wokhulupirira. Mukuona? Chotero izo zimakhala mkati mwa kuyitana kwa Mulungu, kusankha kwa Mulungu.

<sup>16</sup> “Ndipo aliyense asanabadwe, Mulungu anati, ‘Ndamukonda Yakobo ndipo ndamuda Esau,’ aliyense wa iwo asanabadwe.” Chotero momwe ife tikuyenera kumverera. Winawake amene Mulungu wayankhula nawe ndi kukuitanira iwe kuti ubwere ku gome Lake ndi kunyumba Kwake, ndi kudzakhala mwana wamwamuna Wake kapena mwana wamkazi, palibe chinthu

chachikulu chonga chimenecho.

<sup>17</sup> Anyamata awiri awa, ngati ife tingazindikire chikhalidwe chawo, mmodzi wa iwo anali munthu wauzimu, ameneyo anali Yakobo. Ndipo munthu wachithupithupi anali Esau. Koma awiri onsewo anali achipembedzo. Ndipo chinthu chomwecho chimene chakhala chikuchitika monse kudutsa mu m’badwo, wachithupithupi ndi wauzimu.

<sup>18</sup> Esau ankaimira munthu wapadziko lapansi, wachibadidwe, wotsamira ku chipembedzo, koma wosatha. Izo munalibemo mwa iye kuti achite zimenezo. Iye sakanatha kuchita zimenezo. Iye sanali konse mwa iye kuti athe kukwera modutsa zinthu za mdziko, chinthu chachithupi.

<sup>19</sup> Koma, Yakobo, zinali zophweka basi kuti iye achite izo. Tsopano, Yakobo, cholinga chimodzi chimene Yakobo anali nacho, ndipo icho chinali chakuti iye ankakhumba ukulu wobadwa umenewo, zinalibe kanthu momwe iye anawupezera iwo, basi kuti iye anawupeza iwo.

<sup>20</sup> Ndipo mzimu umenewo wa kubadwa kumodzi uko ukuimiridwabe mdziko lero, ndipo ukufika pachimake tsopano: wokhulupirira wauzimu; ndi munthu wachithupi, wokhulupirira wachithupi. Palibe amene anganene kuti awiri onsewo sanali achipembedzo. Iwo anali. Iwo sananene kuti wina ankatumikira “fano” ndipo winayo “Mulungu.” Awiri onsewo anali antchito a Mulungu.

<sup>21</sup> Tsopano, mvetserani mwatcheru ku Malemba tsopano pa phunziro ili, chifukwa ine ndikutsimikiza izo zikuthandizani inu. Mukuona? Tsopano, “Si onse amene amati, ‘Ambuye, Ambuye’ adzalowa mmenemo, koma iye amene akuchita chifuniro cha Atate Anga amene ali Kumwamba.”

<sup>22</sup> Tsopano ngati inu mungazindikire, Yakobo anali ndi chinthu chimodzi chimene iye ankachifuna, chifukwa, molingana ndi Mawu, madalitso ndi—chinthu chabwino chinali mu ukulu kubadwa. Ndipo, Yakobo, icho chinali cholinga chake chokhacho, chinthu chokhacho chimene iye anali nacho mmalingaliro chinali “tenga ukulu wakubadwa umenewo.” Ndipo Esau anawunyoza iwo. Iye amene anali nawo kwenikweni, anawunyoza iwo, kapena iye ankachita nawo manyazi. Koma Yakobo ankawufuna mosalabadira momwe akanawupezera iwo, iye ankawufuna iwo.

<sup>23</sup> Umo ndi momwe ziliri ndi wokhulupirira wauzimu lero. Iye samasamala momwe inu mukumusekera iye, kuchuluka kwa momwe mukumusereulira, momwe iye amachitira mopusa ndi malingaliro achithupi. Chokhumba chake chokhacho chimakhala ukulu wakubadwa. Iye akufuna kuti akafike kwa Mulungu, chifukwa zinabadwira mwa iye. Iye sangachitire mwina.

<sup>24</sup> *Yakobo* amatanthauza “wonyenga” kapena “wonama.” Koma atawupeza ndi kudzakhala nawo ukulu wakubadwawo, iye anasinthidwa. Ndicho chachithupi, kusintha. Iye ankatchedwa nthawi imeneyo, Yakobo, “kalonga ndi Ambuye,” amene analimbana ndi Iye.

<sup>25</sup> Wokhulupirira wachithupithupi lero, “Oh, bola ngati ine ndimapita ku tchalitchi ndi kumachita chimene chiri choyenera, kodi izo zimapanga kusiyana kotani?” Limenelo ndi gulu la Esau. Iye amasekabe ndi kunyoza ukulu wakubadwa, Iye samausamala. Koma Yakobo ankawukonda iwo.

<sup>26</sup> Ndipo mwamuna wauzimu lero, ndi mkazi wauzimu, amene ali wosankhidwa, wokonzedweratu ndi Mulungu kuti abwere ku Moyo Wamuyaya, ngati iwo akuyenera kugulitsa chirichonse chimene iwo ali nacho, ngati iwo akuyenera kuchotsa dzina lawo pa bukhu la mpingo uliwonse mu fuko, iwo amawufunabe ukulu wakubadwa umenewo. Ndi chinthu chokhacho chimene chimakhala chofunikira kwa iwo, “nkungotenga ukulu wakubadwa umenewo,” ndizo zonse. Ziribe kanthu momwe, mlingo umene iwo akuyenera kubwerapo, ngati iwo akusowekera kugwada pa guwa ndi kulira, boo-hoo, ngati iwo akuyenera kuthamanga kudutsa—a—malo ndi kubwerera ndi kudzakonza zinthu, ndi kugulitsa zomwe ali nazo, kapena—kapena kupereka zonse zomwe ali nazo ndi kukhala mwendamnjira ndi mlendo, izo zimakhala zopanda ntchito. Iwo akufuna ukulu wobadwa. Ndizo zonse zimene iwo amakondweretsedwa nazo, ukulu wobadwa. Tsopano, musawanene anthu amenewo. Iwo sangachitire mwina. Iwo anakonzedweratu ku zimenezo, anasankhidwiratu ku zimenezo.

<sup>27</sup> Ndipo kenako ife tikuwona kuti awiri awa, anthu achithupi ndi auzimu, umo momwe izo nthawizonse zinkachitikira. Umo ndi momwe ziliri lero. Izo nthawizonse zakhala ziri chomwecho.

<sup>28</sup> Kaini ndi Abele. Mmunda wa Edeni, pamene Edeni analengedwa, munali mitengo iwiri yoti munthu asankhepo. Umodzi, iye amadzakhala wanzeru; winawo, iye amadzakhala Moyo. Panali anyamata awiri, Kaini ndi Abele, awiri onse a iwo achipembedo. Mmodzi wa iwo ankafuna Moyo Wamuyaya, ndipo anapereka kwa Mulungu, mwa chikhulupiriro, nsembe yopambana kwambiri kuposa Kaini. Choyimira changwiwo cha mipingo lero: mpingo wathupi, mpingo wauzimu. Ndipo palibe kukayikira koma kuti ndikuyankhula kwa magulu awiri onsewo pakali pano, ndipo mwinamwake mwa tepi ndidzayankhula kwa mateni amasauzande a iwo.

<sup>29</sup> Koma, taonani, mpingo wachirengedwe, ndi mpingo wachithupithupi basi. Iwo sangakhoze konse kukhala pamwamba pa chinthu chaching’ono chimenecho cha “Ine ndinajowina mpingo. Ngati ine ndimapita ku tchalitchi, ngati ine ndimachita mopambana momwe ine ndingathere, ndizo

zonse zimene Mulungu amafuna.” Tsopano, ndicho chinthu chomwecho chimene Kaini ankachita. Iye anapita ndipo anakapanga guwa. Iye anakapanga nsembe, anabweretsa zipatso za mnthaka. Ndipo iye anati, “Ndi izi apa, Mulungu. Ndizo zonse zomwe ndapeza. Mutenge izo kapena muzisiye izo.” Umo ndi momwe wokhulupirira wachithupithupi amakhulupirira lero. “Ambuye, ndipita ku tchalitchi. Ndikajowina gulu labwino kwambiri limene ndingakalipeze. Ndikapereka zopereka zanga ku tchalitchi. Ndikachita chimene chiri cholondola. Tsopano, izi ndizo zonse zomwe ine ndingachite. Ndikathandizira kumugulira makala mkazi wamasiye. Kapena, ndikawapatsa ana zovala.” Izo zonse ndi zabwino, palibe choti ndinganene motsutsa izo. “Koma ndi zimenezo, ndizo zonse. Ngati Inu mukufuna izo, tengani izo; ngati Inu simutero, Inu simukusowa kuti mutenge izo.” Tsopano, ndiwo mawonedwe a mpingo wachithupithupi lero.

<sup>30</sup> Koma mpingo wauzimu! Abele, mwa vumbulutso, mwa chisomo, iye ankawona kudutsa zimenezo, ndipo mwa chikhulupiriro iye anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana kwambiri kumuposa Kaini. Ndipo izo zinachitira umboni chirungamo chake, Mulungu.

<sup>31</sup> Chinthu chomwecho chinachitika mwa Ishmaeli ndi Isaki. Mmodzi anali wa thupi, ndipo winayo anali wa Mzimu. Mmodzi, wa mdzakazi; winayo, wa mfulu.

<sup>32</sup> Icho chinachitika chinthu chomwecho mu Israeli ndi Moabu, mipingo iwiri yayikulu ikubwera pamodzi. Ndipo pamene Israeli ankafuna kupita ku malo awo olonjzedwa, mpingo wauzimu, anthu a Yakobo, Israeli panjira; Anthu a Esau anakumana nawo iwo, Moabu, mpingo wamphamvu. Ndipo mtsogoleri wamkulu wa mpingo, Balamu, anatsika kuti adzamutemberere m'bale wake, koma anapeza kuti sangathe kumutemberera m'bale wake. Iye analephera, ndi kuchita khungu kwa maso ake, kuwona dongosolo lokonzedweratu, ilo, ndi kuwawona Mawu a Mulungu.

<sup>33</sup> Choyamba, “Chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva Mawu a Mulungu.” Kenako wokhulupirira amawamva Iwo, amawazindikira Iwo, ndipo amachitapo pa Iwo. Munthu wachithupithupi adzawamva Iwo, phokoso la Iwo, koma ayi. . . *Kumva* kumatanthauza “kuwamvetsa” Iwo. Kuyang'anapo, ndi kuyang'ana pa chinachake; koma *kuwona* izo, ndi “kuzimvetsa” izo. “Pokhapokha munthu atabadwa mwatsopano, iye sangathe kuwuwona kapena kuwumvetsa Ufumu wa Mulungu.”

<sup>34</sup> Tsopano, apa pakubwera Israeli, akubwera ndi lonjezo la Mulungu, kuti iwo ankapita ku dziko lolonjzedwa. Osati achikunja, koma okhulupirira, okhulupirira mwa Mulungu yemweyo amene Israeli anali naye, anatuluka kuti adzayesere kumutemberera m'bale wake, chifukwa iye ananena kuti m'bale

wake ndi, ndithudi anali wosalungama chifukwa iye anachita zinthu zoyipa zambiri. Koma, inu mwaona, iye analephera kuti awone chisankho.

<sup>35</sup> Chinthu chomwecho ndi Esau ndi Yakobo! Esau ankawoneka ngati anali munthu wabwino. Iye anakhazikika ndipo ankachita zinthu zachifundo. Iye—iye ankawasamalira abambo ake okalamba akhungu, ankawapezera iwo nyama ya mtchire ndipo ankawasamalira iwo, ndipo anali mnyamata wabwino. Zinthu zambiri zimene okhulupirira achithupithupi amachita mu mzere wa chipembedzo, kuthandizira mabungwe, ndi—ndi kulipira ngongole za kuchipatala za anthu, ndi zinthu zachipembedzo, koma izo si zimene ndikunena.

<sup>36</sup> Moabu anali wabwino, fuko lopambana, m'bale kwa iye. Ndipo Yakobo anali atachita chirichonse, iye anakhala ali chigawenga; komabe iye anali ndi chinthu chimodzi choti akwaniritse, icho chinali kupeza lonjezo limenelo, ukulu wobadwa umenewo. Apa pakubwera Israeli, ana a Yakobo, ali ndi cholinga chomwecho. Tsopano ndani ati akhale wolondola?

<sup>37</sup> Balamu anamanga maguwa seveni; mu Israeli munali maguwa seveni. Balamu anapereka nsembe seveni za nyama zoyera; Israeli anapereka nsembe seveni za nyama zoyera. Kumeneko, ngati iwo azitenga izo mwamwambo, Moabu anali wachipembedzo basi monga Israeli anali, Esau wachipembedzo basi monga Yakobo anali, ndipo Kaini wachipembedzo basi monga Abele anali. Koma, ndi kusankhidwa kumene kumagwira.

<sup>38</sup> Akhungu bwanji! Momwe ana a Esau aliri akhungu, kuyankhula mwauzimu, Amoabu, ankawayang'anira pansa a Israeli ndipo anati, “Tawaoneni iwo. Iwo si chipembedzo. Iwo ndi gulu la wopanduka. Iwo akukhala mmahema. Ndipo ndife fuko lalikulu. Iwo achita zoyipa. Ndipo iwo alibe bungwe pakati pawo. Iwo akungozungulirazungulira, kutsatira mneneri.” Koma iye analephera kuwona Njoka ya Mkuwa ndi Thanthwe lokanthidwa likupita patsogolo pawo. Iye analephera kuwona gulu lotulutsidwalo, losankhidwa lija likutsatira dongosolo Lauzimu la Mulungu kupita ku dziko lolonjezedwa.

<sup>39</sup> Umo ndi momwe izo ziriri lero. Iwo amati, “Ndi gulu la oyera odzigudubuza. Ndi gulu la anthu omwe ali *ichi*, *icho*, kapena *china*.” Koma iwo amalephera kuwona kuti ndi kutsatira malangizo a Mawu a Mulungu.

<sup>40</sup> Israeli anali panjira yake akupita ku dziko lolonjezedwa. Mulungu, mu Mawu Ake, anapanga lonjezo.

<sup>41</sup> Yakobo, chifukwa chimene iye anasankhira kuti apeze ukulu wobadwa umenewo, mosasamala, iye ankafuna kuti awupeze iwo, chifukwa choti iye ankadziwa kuti ukulu wobadwawo unali ndi madalitso. Iwo unkasungira moyo. Iye sanasamale momwe



iwo ungabwerere, basi bola iye wawupeza iwo. Icho chinali chinthu chenichenicho. Ndi motani momwe iwo unabwerera, zinalibe kanthu. Iye ankawufuna iwo. Ndipo akuyenera kukhala nawo iwo. Ndipo iye anawupeza iwo. “Odala ndi iwo akumva njala ndi ludzu la chirungamo, iwo adzakhuta.” Iye anali panjira yake, ndipo iye ankatsatira iwo, ndipo iye analandira iwo.

<sup>42</sup> Israeli anali pa ulendo wake waku dziko lolonjezedwa. Ziribe kanthu ndi Amoabu angati ndi matemberero amene iwo anayesera kuwayika pa iwo, iwo anapita molunjika ku dziko lolonjezedwa.

<sup>43</sup> Ndipo lero simudzatero...ziribe kanthu kuti iwo apeza chilamulo chochuluka bwanji, kutsutsidwa kochuluka bwanji, kuzunzidwa kochuluka bwanji, zinthu zoipa zingati zimene iwo akunena, ndi kangati iwo akukutchulani “woyera wodzigudubuza,” ndi kangati iwo akunena zoipa zimenezo, mpingo udzasunthirabe chitsogolo. Iwo ukuyenera kutero. Ndi kukhala mu Mawu a Mulungu.

<sup>44</sup> Nthawi ina mafumu awiri anabwera pamodzi. Mmodzi wa iwo anali Ahabu, woyipa, winayo anali Yehosafati; mpingo wauzimu, mpingo wachithupithupi.

<sup>45</sup> Ahabu anali wokhulupirira wammalire. Iye anali ndi aneneri. Iwo sanali achikunja. Iwo sanali opembedza mafano. Iwo anali aneneri achi Israeli, koma onse ankaphunzitsidwa ndi kudyetsedwa ndi kuvekedwa ndi Ahabu mfumu. Iwo anakhala ngati malo amene iwo anali ndi zochirikizidwa zonse za ndale.

<sup>46</sup> Yehosafati anabwerapo, akubwera kumusi, anapanga mgwirizano, chimene chiri cholakwika.

<sup>47</sup> Inu musamagwirizane konse ndi osakhulupirira. Sitikuyenera konse, mwanjira iliyonse, kuyika mayina athu mmabuku a mipingo imene simakhulupirira Uthenga wathunthu. Ayi! Mudzalowa nazo mmavuto.

<sup>48</sup> Ndipo iwo analowa nazo mmavuto. Ndipo mwamuna wolungama uyu anati, “Kodi sitikuyenera kufunsira kwa Ambuye poyamba, ndi kupeza ngati tikuyenera kupita ku Ramoti-Giliadi?”

<sup>49</sup> Tsopano taonani momwe chochitikacho chinkawonekera changwiwo. “Ndife eni ake a Ramoti-Giliadi. Ndi chuma chathu, ndipo Asiriya anatenga ilo kwa Mulungu wamoyo. Kodi sitipita ndi kukalitenga dziko ili?” Ndipo iye anapanga kuyankhulako kukhala kokongola kwambiri, ndi kovomerezeka kwambiri, ndi kolungama kwambiri, mpaka Yehosafati anatsatira izo.

<sup>50</sup> Ndipo, lero, amuna akhoza kuyima pa guwa ndi luntha ndi kuyankhula, ndi maphunziro, mpaka iwo nkumakhoza kufotokozera Mphamvu ya Mzimu Woyera mophotchola kutali ndi Baibulo. Iwo akumakhoza kuwafotokoza machiritso Auzimu mophotchola. Iwo akhoza kukufotokoza kuyankhula mmalirime

ndi kutanthauzira, iwo akhoza kuwufotokoza ubatizo wa Mzimu Woyera, kwa tsiku lina.

<sup>51</sup> Koma munthu amene ali wosankhidwa ndi Mulungu, munthu . . . “nkhosa Zanga zimalidziwa Liwu Langa.” Inu muli ndi kusankha kwa Mulungu kuja pa inu, sizidzakupunthwitsani konse.

<sup>52</sup> Yehosafati anati, mfumu yolungama inati, “Kodi kulibe mneneri, amene ife tingathe kufunsirako kwa Ambuye?” Ahabu ankapita popanda izo.

<sup>53</sup> Umo ndi momwe mpingo wachithupithupi ukuchitira lero. Oh, iwo ali ndi maseminare odzaza ndi alaliki, amuna aakulu, mapurofesa aakulu, aluntha, anzeru, ochenjera, oh, mai, kutali kudutsa—nzeru za mpingo thu- . . . kapena mpingo wauzimu.

<sup>54</sup> Mu masiku a Nowa, mu masiku amenewo, tayang’anani pa mpingo wachithupithupi. Kodi iwo anali chiyani? Asayansi, amisiri, amuna anzeru. Koma osankhidwa, Enoki ndi Nowa, anali abusa ndi alimi, odzichepetsa, osaphunzira, opanda nzeru, koma ankamudziwa Mulungu wawo; chinachake mwa iwo, chinkasuntha, chinkaitana. Tifika kwa izo pakapita kanthawi.

Tsopano, chotero Yehosafati anati, “Kodi kulibe mneneri?”

<sup>55</sup> Oh, ndithudi, achithupithupi ali nawo iwo. “Ndithudi, ife tiri nawo. Ine ndiri ndi seminare kumusi kuno, yodzaza ndi iwo.”

<sup>56</sup> Anabweretsa foro handirede. Tsopano, awa si achikunja. Iwo ndi opembedza Yehova Mulungu. Anabwera, ndipo anati, “Tiyeni tikhale ndi kanthawi ndipo ife tinenera.” Ndipo chotero iwo onse anasonkhana pamodzi. Ndipo iwo anabwerera ndi, “Mawu a Ambuye,” ndipo iwo anati, “PAKUTI ATERO AMBUYE.” Aneneri achi Israeli. “PAKUTI ATERO AMBUYE. Pitani, Ambuye ali nanu. Ndipo inu mukatenga Ramoti-Giliadi, chifukwa iye ndithudi ndi wa Israeli.” Ndipo mmodzi wa akuluakulu anadzipangira nyanga ziwiri zazikulu za chitsulo, monga zoimira, ndipo iye anapita akukankha. Iye anati, “Ndi ichi inu mukankha Israeli. . . kapena mukawakankhira Asiriya kuchoka ku Ramoti-Giliadi.”

Koma, Yehosafati, chinachake mwa iye!

<sup>57</sup> Oh, ine ndikuyembekeza kuti Mulungu azibweretsa izi ku mtima wanu. Si chinthu chimene mungadziphunzitse nokha. Si chinthu chimene mungawerenge nokha. Ndi chimene Mulungu, mwa kusankha, amakuchitirani inu. “Si iye amene athamanga kapena iye amene awonetsa- . . . Ndi Mulungu amene amawonetsera chifundo.”

<sup>58</sup> Yehosafati anati, “Iwo ndi amuna ovala bwino.” Sindikukaikira iye ananena chinachake monga ichi, “Iwo ndi aluntha, ndipo amuna anzeru kwambiri amene ndinawamvapo. Iwo ndi ophunzira mpaka pano. Mayimidwe awo ndi mgwirizano

umodzi. Iwo ali ndi umodzi waukulu pakati pawo. Ndipo iwo ndi anzeru, ndipo ali ndi Choonadi chochuluka kwa iwo.”

<sup>59</sup> Kulakwitsa konse kumakhala ndi Choonadi. Bodza lalikulu limene linanenedwapo linali ndi nainte-...[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. peresenti Choonadi mwa ilo, bodza limene Satana anamuuzza Eva.

<sup>60</sup> “Oh, ndi Choonadi chochuluka mu chimene iwo akunena, koma kodi palibenso wina?”

<sup>61</sup> Chabwino, kodi mukuganiza kuti munthu uja ananena chiyani? “Pamene ife tiri ndi foro handirede pano, mwa anzeru, apamwamba? Iwo sali kunja kuno mu chipululu akuthamanga mozungulira ali maliseche mwatheka, ndi chikopa cha nkhosa chitakulungidwa pa iwo, kapena chinachake. Ndi amuna amene ine ndawadyetsa, ndawaphunzitsa. Iwo si amuna amene sadziwa ma ABC awo. Iwo ndi masikolala, ndipo iwo amadziwa chinthucho. Iwo amakhala, usana ndi usiku, akuwerenga mipukutu ndi uneneri. Iwo amadziwa chimene chiri cholondola. Ine ndawakonzekeretsa iwo. Ndipo iwo ayima pano ndi mgwirizano umodzi, foro handirede a iwo, akuti, ‘Pitani, Yehova ali nanu.’”

<sup>62</sup> Koma ngati ine ndikanakhoza kuwerenga malingaliro a Yehosafati maminiti pang’ono, “Pali chinachake chimene sichikuvomereza,” iye amakhoza kunena. “Pali chinachake basi chimene sichikuwoneka bwino. Kodi kulibe winanso m’modzi, kwinakwake?”

<sup>63</sup> “Oh,” iye anati, “inde, alipo mmodzi wina, koma iye si wa bungweli. Iye ndi munthu wantundu wosiyana. Iye ndi wopanduka basi.” Iye ali ngati Yakobo. “Koma ife tikhoza kumufunsa. Iwo amati iye ndi mneneri. Koma ine ndimakaikira izo, chifukwa iye nthawizonse amanditemberera ine, amanena kuti *ichi, icho*, kapena *chinacho*, kapena iye samanenera zabwino za ine.” Iye angatero bwanji? Mukuona?

<sup>64</sup> Chotero iwo anati, “Tiyeni tikamutenge iye. Iye ndi mwana wa Imla.” Chotero iwo anapita ndipo anakamutenga iye.

<sup>65</sup> Ndipo winawake anakomana naye panjira, anati, “Tsopano, iwe ukanene chinthu chomwecho chimene iwo akunena. Iwe ukuyenera kuvomerezana nawo mgwirizanowo. Ngati sutero, tsoka kwa iwe!”

<sup>66</sup> Iye anati, “Ine ndikangonena chimene Mulungu wayika mkamwa mwanga kuti ndikanene, ndipo palibe chinanso.”

<sup>67</sup> Kenako iye atafika kumeneko, ndipo iwo anamupatsa iye usiku umodzi, iye anati, “Pitani kumeneko, koma ine ndinawona Israeli atamwazika ngati nkhosa zopanda m’busa.”

Ndipo Ahabu anati, “Kodi ine sindinakuuzeni inu?”

<sup>68</sup> Tsopano, pali foro handirede akutsutsana ndi mmodzi. Amuna foro handirede ophunzitsidwa, anzeru, ophunzira,

aluntha akutsutsana ndi mbuli imodzi yaing'ono, monga ife tikanamutchulira iye, Mikaya. Munthu mmodzi, komabe munthu mmodzi ameneyo anali ndi Mawu a Ambuye, zimenezo zinapanga kusiyanita. Aliyense wa iwo anali wabodza, izo zinatsimikizidwa kukhala zabodza. Nchifukwa chiyani Mikaya anali wosiyana kwambiri? Kodi iye ankayenera kukhala wosauka, kuti akhale wosiyana? Ayi. A... Chimene chinamupanga Mikaya kukhala wosiyana, iye anakhala ndi Mawu. Mawu a Mulungu ndi chimene iye anakhala nacho.

<sup>69</sup> Tsopano kunalonjezedwa kuti, mmasiku ano, “Mulungu adzatsanulira Mzimu Wake.” Zinalonjezedwa ndi Danieli kuti, “Anthu, mmasiku amene mwala udzagunde fano ku phazi, anthu amene amadziwa Mulungu wawo adzachita zazikulu.” Uneneri pambuyo pa uneneri! Ndipo maseminare onse, dziko, sangathe kuzichotsa izo. Mulungu adzachita izo, mulimonse, ndipo anthu azitsatira izo. Mukuona? Wachithupithupi ndi... Mpingo wachithupithupi ndi mpingo Wauzimu. Inu mwaona, Mawu amapanga kusiyanita.

<sup>70</sup> Izo ndi zomwe Yakobo anaganiza, “Ndipo ziribe kanthu chiyani, ine ndikudziwa sindingathe kudalitsidwa pokhapokha nditatenga ukulu wobadwa umenewo. Ukulu wobadwa umenewo ndi umene ndikuyenera kuwugwira.”

<sup>71</sup> Ndipo, koma Esau anakadana nawo iwo, ndipo ana ake amachita chinthu chomwecho, komabe, mpaka lero. Iwo amadana nawo. Nthawizonse zakhala ziri chomwecho.

<sup>72</sup> Nthawizonse pakakhala chitsitsimutso, nthawizonse chimatulutsa mapasa. Iyi ndi ndemanga yamwano, koma ndi zoono. Pamene panakhala kubadwa kuchokera mwa, Isaki ndi Rebekah, iko kunatulutsa mapasa. Pamene dziko linalengedwa, linabala mapasa, mitengo iwiri. Ndipo pamene Kaini ndi Abele anabadwa, izo zinabala awiri. Pamene Ismaeli ndi Isaki anabadwa, izo zinabala awiri. Ndipo pamene Esau ndi Yakobo anabadwa, izo zinabweretsa awiri. Mmodzi wa iwo, wachirengedwe (mmodzi wa iwo, wa padziko lapansi); winayo, Wauzimu. Ndipo wina ankayang'ana pa chirengedwe, zaluntha; winayo ankayenda mwa Mzimu. Nthawizonse zakhala ziri chomwecho. Pamene mpingo wa Lutheran unatulukira...

<sup>73</sup> Tiyeni titenge Chipentekoste, poyamba. Tayang'anani pa kubadwa kwa Chipentekoste. Icho chinabweretsa chitsitsimutso chachikulu, champhamvu chimene chinasesa dziko lodziwika, Chipentekoste. Sipanapite nthawi yaitali itatha Pentekosite mpaka ngakhale Paulo anati, kuti, “Padzakhala amuna omwe adzawuke pakati pawo, ndi zinthu zokhotakhota, ndipo adzawatembenzira anthu kutali ndi Mulungu.” Ndipo ndicho ndendende basi chimene iwo anachita. Chimabala ziwiri.

<sup>74</sup> Pamene mpingo wa Lutheran unabadwa, Martin Luther anabweretsa chitsitsimutso chauzimu. Sipanatenge nthawi

yaitali mpaka apa panadzabwera Esau, kumbuyo kwake komwe, ndipo anachipanga icho bungwe. Ndipo icho chinatulutsa ziwiri.

<sup>75</sup> Ndiye zitatha izo, panadzabwera Amethodisti, John Wesley, chitsitsimutso chاوزimu. Ndipo zitatha izo, panadzabwera bungwe, linapanga icho bungwe. Ndipo linatulutsa ziwiri.

<sup>76</sup> Ndipo zitatha izo, kunadzabwera Pentekoste, chitsitsimutso. Ndipo tsopano iwo apanga bungwe icho, ndipo tsopano iwo akukhazikika mu bungwe. Ndipo ilo likupanga ziwiri.

<sup>77</sup> Koma mbewu yauzimu ija ya Mulungu wamoyo, ngakhale iyo ikuyenera kukhala mwendamnjira, ngakhale iyo ikuyenera kukhala woyendayenda, iyo nthawizonse imayambitsa kulekana. Esau sanakhalitse nthawi yaitali ndi Yakobo. Yakobo atangolandira ukulu wobadwa (Mulungu alemekezeke), zinayitanira kulekana. Ndipo pamene mwamuna...Ine sindikusamala kuti ndiwe wa mpingo wanji, ngati uli wachithupithupi, ndi oyanjana nawo amene inu mumayenda nawo, anthu amene mumasewera nawo makadi, ndi mabungwe anu a mabuku, ndi zina zotero; pamene inu mulandira ukulu wobadwa, chinachake chimene chiri pansu mu mtima mwanu chimene chiri ndi njala ya Mulungu, pamene inu mulandira icho, icho chimayitanira ku kulekanitsidwa. “Tulukani pakati pawo, ndipo patukani, atero Mulungu.” Kulekana!

<sup>78</sup> Mpingo ukukhazikika pansu. Mwaona, iwo sungapitirire. Esau anali woyimira wabwino wa wokhulupirira wathupi lero, wosatha kuligonjetsa dziko lapansi. Iye samagonjetsa zinthu za mdziko. Iwo amakondabe kusewera kwawo, kuvina kwawo, zozipaka zawo ndi, akazi, pankhope zawo, ndi—ndi kumadula tsitsi lawo ndi—ndi kumavala zovala zazing’ono zakale zazifupi izi; ndipo—ndipo munthu amakonda kupita kuzipinda zamadziwe, ndi—ndi kumakasuta ndudu, ndi kumakanena nthabwala zazing’ono zonyansa; ndipo nkumakhalabe a mpingo. Iwo sangakhoze konse kugonjetsa zinthu zimenezo. Ngakhale Esau sangathe. Komabe, kuti akhale wachipembedzo, iye ankayenera kukhazikika ku lingaliro laluntha. Ndicho chinthu chomwecho chimene mpingo ukuchita lero. “Tikhala bungwe. Tidziyika tokha pamodzi. Ife tipanga fuko, kapena kagulu, kapena chinachake chonga icho.”

<sup>79</sup> Ndipo umo ndi momwe mpingo ukusunthira lero, wauzimu ndi wachithupi, zikadali zomwezo. Izo sizinasinthe, ndipo sizidzasintha konse.

<sup>80</sup> Chiyero cha Mulungu. Mulungu, pokhala Mulungu, amawonetsera zimenezo, Iyemwini. Ngati kukanakhala kuti kunalibe wochimwa, apo sipakanakhala konse...Iye sakanakhala konse Mpulumutsi. Koma Iye anali Mpulumutsi pa chiyambi, chotero panalibe kanthu kotayika. Ndipo zikhumbo Zake Zomwe monga kukhala Mpulumutsi, zinkawonetsera wochimwa, pankayenera kukhala chinachake choti

chipulumutsidwe. Pasanakhale chirichonse chopulumutsidwa, pankayenera kukhala chinachake chotayika. Ndi chirungamo Chake ndi chiyero Chake! Ngati pakanati sipanakhalepo a—munthu wodwala, Iye sakanakhala konse mchiritsi. Koma kuyambira pachiyambi, ndi pa chiyambi, Iye analipo chiyambi chisanakhalepo. Iye anali mchiritsi. Chotero panalibe kanthu kodwala, chotero izo zinam'bweretsa munthu wodwala, kuti Iye adzathe kuwachiritsa iwo, kuti zidzamupange Iye kukhala mchiritsi.

<sup>81</sup> Kuchokera mu Dera Loyera lomwelo uko kumene kunachokera chipulumutso, kunachokeranso matemberero. Kuchokera mwa mayi yemweyo ndi abambo omwewo anawonetsera Yakobo, anawonetsera Esau. Mukuona? Ndi Mulungu. Iye sangasinthe dongosolo Lake. Iwo akuyenera kupita chimodzimodzi basi. Chirengedwe chonse chidzagwirizana momwemo. Icho chikuyenera kutero. Inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza? Kuchisunthira icho mkati momwe. Pakuyenera kukhala winawake wotaika, kuti apulumutsidwe. Ndipo ngati pakanati pasakhale, Iye, Wake. . . Iye pokhala Mpulumutsi anapanga izo. Kuya kuyitanira ku Kuya.

<sup>82</sup> Monga mnyamata wamng'ono amene ndimayankhula za iye nthawi zonse, akudya zofufutira pa mapensulo, ndi pedulo lanjinga, iye ankasowekera safu. Ndipo bola ngati munali chinachake mmenemo cholakalaka safu, pamayenera kukhala safu penapake, poyamba, apangidwe. Pankayenera kukhala safu iye asanakhale ndi chikhumbocho. Ndipo iye, safu, anamulozera iye, ndiye iye anabwerera ku safayo.

<sup>83</sup> Umo ndi momwe Mulungu aliri Mpulumutsi. Ndipo pankayenera kukhala chinachake choti chidzatayike, kuti Iye adzachipulumutse, kuti chidzamupange Iye Mpulumutsi. Ndizo zonse zimene zikuchita, ndi kusewera Mulungu. Chirichonse, zonse ziri mwa Iyeyo; osati mwa mlaliki, osati mu mpingo, osati mu bungwe, koma mwa Mulungu, kuti kusankha kukhoze kuyima mwangwiro. Mukuona? Izo ziri mwa Iye. Eya. Achilutera. . .

<sup>84</sup> Ndiyeno ife tikuwona kulekana kwina, uko kunali Abrahamu ndi Loti. Iwo anali abale. Koma Loti anali woganiza mwathupi. Iye nthawizonse ankapita kumakafuna chinthu chachikulu, chinachake chokhala ndi zonyezimira zochuluka pa icho. Monga ngati nyani, monga ine ndinganenere, nthawizonse amafikira chinthu chowala. Mzimu umenewo sunawachokere anthu, lero. Iwo amafikira kwa. . . Iwo amapita ku mzinda, ndipo iwo sangabwere ku kanyumba kakang'ono monga chonchi. Mukuona? Iwo amafuna tchalitchi chachikulu kwambiri chimene chiripo mu mzinda, m'busa waluntha kwambiri, kumene anthu ovala bwino amapita, kumene ameya amapita, ku mzinda. Ukanali mzimu wa Esau womwewo. Analidi ndi ukulu

wobadwa, kuyamba ndi kuyamba, amadzitcha okha Mpingo, koma iwo anawutaya iwo chifukwa iwo amawunyoza Iwo. Inu simungakhoze kuwapangitsa anthu amenewo kuti agwade pa maondo awo, ndi kulira ndi kupempha kwa Mulungu, ndi kupita kunja ndi kukakhala ndi msonkhano wa machiritso, ndi kupirira chizunzo cha dziko, kulandira Mzimu Woyera. Ndipo iwo—iwo sangachite zimenezo. Iwo amanyoza izo. Iwo amazitcha izo “gulu la oyer a odzigudubuza.” Basi chimene Baibulo linanena kuti iwo akanadzachita. Iwo amachita izo chifukwa icho ndi chikhalidwe chawo. Ndi chikhalidwe. Monga khwangwala ndi nkunda, zikhalidwe ziwirizo. Izo zimafuna icho chifukwa ndi chimene izo ziri. Iwo sadzachiwona konse (sadzatero) chinacho, chifukwa iwo sanabadwe kuti adzachiwone icho.

<sup>85</sup> Ndipo mmodzi winayo, inu simungakhoze kumuchotsa iye kwa izo, chifukwa ndi kusankha kwa Mulungu. Iye anabadwa kuti adzakhale mwamuna wauzimu kapena mkazi wauzimu. Chinachake mwa iye chimaitanira icho. Oh, ine—ine ndikuyembekeza kuti izi zikufika pamalo amene ife tingathe, inu mukhoza kuona chimene ine—ine ndikutanthauza, pomalizitsa izo tsopano. Tsopano Abrahamu . . .

<sup>86</sup> Kumbukirani, nthawi yonse pamene iwo anali oyanjana pamodzi, mpingo wachithupithupi ndi mpingo wauzimu, iwo sanalandire konse mdalitso. Yakobo sanadalitsidwe konse mpaka iye atadzipatula yekha kwa Esau. Ndipo Abrahamu sanadalitsidwe konse mpaka iye atadzipatula yekha kwa Loti.

<sup>87</sup> Loti anali ndi misonkhano yake yaying’ono ya mapemphero mu mpingo wake kumusi uko, anawaphunzitsa ana ake aamuna ndi aakazi, ndi iwo. Koma iye ankakhala moyo woterowo, mpaka, pamene iye anayamba kuyankhula za kutha kwa nthawi, iwo anamuseka iye.

<sup>88</sup> Chinthu chomwe chomwecho lero! Iwe ukayankhula za machiritso Auzimu ndi mphamvu ya Mulungu, ndi zina zotero, iwo amaziseka izo. Ndi mzimu womwewo. Ndiyo mizimu iwiri yayikulu, mwachipembedzo, yaligwira dziko; wokhulupirira ndi wosakhulupirira, wokhulupirira ndi wodzipangitsa-kukhulupirira, mmodzi akutsanzira mzake. Tsopano pamene Abrahamu anadzipatula yekha . . .

<sup>89</sup> Kodi inu munazindikira Yesu? Mukuyankhula Kwake za Kudza, Kudza kwachiwiri, Iye anati, “Monga zinali mmasiku a Nowa, iwo adzakhala akudya, akumwa, akukwatira, ndi kukwatiwa.” Koma pamene Iye anayankhula za masiku a Loti, Iye sananene kanthu za izo. “Monga masiku a Loti,” izo ndi za vumbulutso.

<sup>90</sup> Onani chimene chinachitika mmasiku a Loti. Uko kunali Loti kumusi uko mu Sodomu, wokhazikika bwino, mwaluntha, anakhala a, mmodzi wa akuluakulu a mzinda, woweruza, ankakhala pa zipata ndi kumaweruza anthu. Mkazi wake anali

wa magulu onse amene analipo amu mzindawo. Ndipo ana ake aakazi, ndi onse a iwo, anakwatiwa pakati pa otchuka, aluntha, ophunzira apamwamba, anzeru, aluntha. Ndipo Abrahamu ankakhala mu hema pansu pa mtengo wa mthundu. Koma tsiku lina onse anachezedwa.

<sup>91</sup> Ndipo panali mlaliki waluntha anapita uko ndipo anakalalikira, ndipo anawaitanira iwo kunjira. Tayang'anani pa—tayang'anani pa uthenga, "Tuluka," iye anatero kwa Loti.

<sup>92</sup> Ndipo iye sakanaitanidwa konse kukadapanda chifundo cha Abrahamu. Anati, "Kodi ndingakapeze anthu fifite, kodi Inu mukawasiya iwo? Kodi ndingakapeze anthu sarte? Kodi ine ndinga. . . Ngati ndingakapeze teni?" Umo ndi momwe iye akanapitira. Ndipo Iye sanathe kupeza ngakhale teni mwa iwo.

<sup>93</sup> Nzosadabwitsa, "Monga zinali mmasiku a Nowa." Kumbukirani, Nowa sanali woyimira Mpingo; Enoki anali, amene sanadutse mu chisautso, koma anasanthulitsidwa chisautso chisanayambike. Enoki anapita Kwawo, iye sanadutse mu chisautso. Nowa anadutse.

<sup>94</sup> Tsopano, penyani mwacheru tsopano pamene ife tikusunthira mmwamba mu ichi. Penyani mtundu wa chizindikiro chimene Abrahamu ndi banja lake anali nacho. Iwo anapeza Chauzimu. "Abrahamu!" Kodi Iye anadziwa bwanji kuti iye anali Abrahamu? "Ali kuti mkazi wako, Sarah?" Kodi Iye anadziwa bwanji kuti iye anali wokwatira, kapena anali ndi mkazi, Sarah?

"Iye ali mu hema."

<sup>95</sup> Tsopano, Mwamuna atakhala pamenepo, akudya nyama, akumwa mkaka, ndi kudya buledi wa chimanga. "Alikuti, alikuti mkazi wako, Sarah?" Kodi Iye anadziwa bwanji chinthu chimenecho? Kodi Iye anadziwa bwanji izo? Taganizani za izo. Inu mumatcha. . . Inu anthu auzimu, mulole izi zilowe mwa inu. Kodi Iye anadziwa bwanji izo, pamene Iye ankachita monga mlendo, fumbi pa zovala Zake?

Ndipo pamene Abrahamu anati, "Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu."

<sup>96</sup> Ndipo Iye anati, "Ine ndikuti. . ." "Ine, ine," mlowammalo waumwini. "Ine," Munthu uyu, Mulungu akudzizindikiritsa Yekha mu thupi. Mulungu! Abrahamu anamutcha Iye Elohimu. "Ine, Ine ndidzakuyenderani inu. Ine ndidasunga lonjezo Langa. Ndipo molingana ndi nthawi ya moyo, Ine ndidzakuhezzerani inu, ndipo inu mudzakhala ndi mwana uyu amene Ine ndinayankhula kwa inu za iye." Ndipo Abrahamu, handiredede; Sarah, nainte.

<sup>97</sup> Ndipo Sarah, kumbuyo mu hema; pafupifupi foro a mahema aang'ono, hema wamkulu atakhala kumbuyo. Kuseri kwa zinsalu, iye anali akumvetsera. Iye anamva izo. Ndipo



pansi mu mtima mwake iye anamwetulira, anati, “Ine, mkazi wokalamba wa zaka handirede, ndi mbuye wanga,” mwamuna wake, “mbuye wanga, ndipo wokalamba, ndipo nkuganiza kuti tingadzakhale ndi chisangalalo limodzi kenanso, ngati okwatirana achinyamata? Oh, izo zingatheke bwanji?” Ndipo iye anakhala ngati akumwetulira.

<sup>98</sup> Iye anali atatembenezira nsana Wake ku hema. Iye anati, “Nchifukwa chiyani iye waseka?” Oh, m’bale, ndi inu pamenepo!

<sup>99</sup> Tayang’anani pa mpingo wachithupithupi ukulalikira Uthenga kwa iwo. Billy Graham wamakono ndi iwo kumusi uko akulalikira Uthenga, “Tulukani mmenemo!” Koma kodi iwo anabwera? Ayi. Kwambiri, kwambiri, apang’ono kwambiri.

<sup>100</sup> Penyani gulu la Abrahamu, oyitanidwa atuluke. Tsopano zindikirani. Ndipo Iye anamupatsa iye chizindikiro ichi, ndipo iye anamukhulupirira Iye. Ndipo iye anasowa pamaso pake, ndipo anachokapo. Oh, momwe izo nthawizonse zakhala ziri kulekanitsa, oyitanidwa atulukewo!

<sup>101</sup> Tsopano, mizimu iwiri iyi. Kuti ndifulumire nanu, kuti ndifulumire tsopano kuti ndifike pa malo anga amene ine ndikufuna kuti inu muwone. Magulu awiri amenewa akhala akugwirizana limodzi, monse kudutsa mmibadwo yonse, kuyambira pachiyambi pomwe pa nthawi; mpingo wachithupithupi, mpingo wauzimu. Iwo akhala akudutsa mu Chipangano Chakale, iwo analipo kudutsa mu Chipangano Chatsopano, ndipo alipobe mpaka pansi lero.

<sup>102</sup> Tsopano, pafupifupi zaka thuu sauzande zapitazo, izo zinafika ku mutu, ndipo zinafika mwa amuna awiri: mmodzi wa iwo, Yesu Khristu; winayo, Yudasi Iskariote. Tsopano, Yesu anagwirizanitsa Kudza, kwa Kudza Kwake kwachiwiri, kuti mizimu iwiri iyi idzakhala yosiyana kwambiri kuposa chimene iyo inali kumbuyo uko. Tsopano apa ndi pamene ine ndikufuna kuti inu muvale zanu—zovala zanu za Ulemelero. Mizimu iwiri iyi idzakhala yosiyana. Chifukwa, Satana anabwera ndipo anadzakhala mwa munthu amene anali membala wa mpingo, Yudasi Iskarioti, anakhala mu mpingo wachithupithupi, ndipo anali bwenzi kwa mpingo nthawi zonse. Koma iye anadzalowa ndipo—ndipo anamunyenga, kapena ankaganiza kuti iye akumunyenga m’bale wake. Iye anabwera ndipo anadzipangitsa kukhala ngati anali mmodzi wa iwo; analawa zinthu zabwino za Mulungu, ankayenda limodzi bwinobwino mu Mzimu, zinkawoneka chomwecho, ankapita ndi kukalalikira Uthenga, ndi kukatulutsa ziwanda. Koma pansi mwa iye, nthawi zonse, iye anali Yudasi, kuyamba ndi kuyamba. Baibulo linati, “Iye anabadwa ali mwana wa chitayiko.”

<sup>103</sup> Tsopano kumbukirani, kunali mpingo wachithupithupi kumbuyo uko, Esau, Afarisi ndi Asaduki.

<sup>104</sup> Koma muoneni munthu uyu amene amadziyesa yekha... Iye adzapita limodzi ndi Uthenga kwa kanthawi, koma sadzafuna basi kuti ayike manja ake mochuluka pa Iwo. Mukuiwona mizimu imeneyo? Yesu anati, “Icho chidzakhala pafupi kwambiri ndi chinthu chenichenicho, icho chidzanyenga Osankhidwa omwe,” Osankhidwa, ngati mungazindikire, “ngati kukanakhala kotheka.” Koma izo sizingatheke. Mwaona, izo zidzanyenga.

<sup>105</sup> Tsopano penyani, osati mpingo wachithupithupi wokha, umene uli kunja uko, mpingo wachizolowezi wachithupithupi, gulu la Esau.

<sup>106</sup> Ife tiri nalo tsopano gulu la Yudasi, limene liri lachinyengo kwambiri, lachinyengo kwambiri, kubwera mmanja omwewo a mdalitso. Chimodzimidzi monga mu Ahebi 6 ndi 10, momwe iye ananenera, “Atapangidwa kamodzi kukhala otengapo gawo ndipo analawa mphamvu za dziko lomwe liri nkudza, ndipo anachita zinthu zonsezi; ngati...ndipo kenako ngati iwo adzalandira chidziwitso cha Choonadi, ndipo kenako ngati iwo adzachokapo mwadala.” “Mwadala,” chimenecho ndi chiyani? “Kuwerengera Magazi a pangano, omwe iwo anayeretsedwa nawo, chinthu chosayera.”

<sup>107</sup> Ndiroleni ndikupatseni inu kufotokozera kwake. Ndi ichi apa. Apa pali munthu, iye ndi munthu wabwino, mnyamata wabwino. Iye wayitanidwa, akumverera mu mtima mwake kuti akufuna kukhala mtumiki. Chabwino, iye akumvomereza Yesu ngati Mpulumutsi wake. Iye ndi mnyamata wabwino, palibe amene anganene kanthu komutsutsa iye. Patapita kanthawi, nkhani ya kuyeretsedwa. Mwamunayo amasilira akayang’ana akazi. Iye...Ziri mwa iye. Mukuona? Ndiyeno, chinthu chotsatira, mwinamwake iye ankasuta, ndipo iye akufuna kusuta. Mwinamwake akufuna kutchova juga. Mwinamwake akufuna kuchita chinthu chinachake choyipa. Iye akudziwa kuti sakuyenera kuchita zimenezo, chotero iye akuti, “O Mulungu, ikani Magazi a Yesu kwa ine, ndipo muniyeretse ine.”

<sup>108</sup> Ndipo iye akuyeretsedwa. Iye akhoza kufuula, kutamanda Ambuye, kuchita zinthu zina, nayenso, kupita kunja ndi kukachita chinthu. Kumbukirani, Yesu ananena kuti mtundu umenewo udzakhlapo pa tsiku limenelo. “Ambiri adzabwera ndipo adzati, ‘Ambuye, kodi ine sindinanenere, kulalikira? Kodi ine sindinatulutse ziwanda mu Dzina Lanu?’” Yesu anati, “Ine sindinakudziwe iwe, iwe wochita kusaeruzika.” Mwaona, ndi amenewo apo.

<sup>109</sup> Tsopano penyani ichi tsopano. Ife tikubwera kudzapanga ka kagawo ka handirede milioni ka tsitsi, mpaka kumapeto kwakuthwa kwenikweni kwa Uthenga, “Lakuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, kupyozza kufikira mkati mwa fupa, ndi Wozindikira!” Aleluya! Mulungu, mulole

izo zipyoze. “Wozindikira wa malingaliro a mmaganizo.” Umenewo ndi Uthenga, Mphamvu ya Mulungu. Mawu a Mulungu owonetseredwa ndi Uthenga.

Inu mukuti, “Baibulo linatero. Ndiwo—ndiwo Mawu a Mulungu.”

<sup>110</sup> Chabwino, Mawu owonetseredwa ndi Uthenga. Uthenga unadza kwa ife osati kudzera mu Mawu okha, koma kudzera mu mphamvu ndi ziwonetsero za Mzimu Woyera, kudzawonetsera Mphamvu, kudzawupangitsa Uthenga kukhala wamoyo.

<sup>111</sup> Pamene ine ndinapita ku India, arkibishopu wa—wa mpingo wa Methodisti anabwera, anati, “Bambo Branham, ife sitikufuna kudziwa kalikonse ka umishonare. Ife timadziwa zochuluka za Baibulo kuposa mmene nonse mungadziwire.” Anati, “Ife tinali mpingo, ndipo tinadzakhazikika kuno zaka thuu sauzande inu musanakhale fuko.” Uko nkulondola. Koma anati, “Ife tamva kuti Mulungu wakuchezerani inu ndipo wabweretsa mpatso imene ingapangitse kuti Baibulo ili likhale lamoyo.” Anati, “Ndi zomwe tiri nazo chidwi.” Oh, mai! Mwaona, mwamuna ameneyo anali mwana, osati mdzukulu, monga David ananenera. Mukuona? “Ife tikufuna kudziwa. Ndi zoonza?”

<sup>112</sup> Ine ndinati, “Ndithudi, izo nzoona. ‘Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.’”

<sup>113</sup> Tsopano, muzindikireni iye, mpingo wachithupithupi ukuzunza mpingo wauzimu. Tsopano, ife tikupeza ndiye kuti Yudas akunyengezera kukhala m’bale, m’bale, ndipo kenako analunjika mmwamba ndipo potsiriza anafika pachimake.

<sup>114</sup> Tsopano penyani mlaliki wamng’ono uyū. Iye akubwera pamalo, iye akuti, “Ambuye, ndakhala ndikuyang’ana pa akazi. Ine sindimayenera kuchita izo. Ine ndakhala, inu mukudziwa, kukhala ngati kuchita zinthu za mdziko. Ine sindikuyenera kuchita izo. Ndakhala ndikuwononga ndalama zanga pa mipikisano ya akavalo. Ine—ine sindimayenera kuti ndizichita zimenezo. Ine—ine ndakhala ndikupita usiku uliwonse ku ziwonetsero za zithunzi. Ine sindimayenera kuti ndizichita zimenezo. Ine ndimasangalala ndi zithunzi zolawula ndi zinthu monga choncho, ndiri ndi zopachika mchipinda changa. Ine sindikuyenera kuti ndizichita zimenezo. Ndizo zinthu za mdziko. Ndiyereetseni ine, Ambuye!”

<sup>115</sup> Ndipo Ambuye anati, “Chabwino, Ine ndichita zimenezo.” Iye akupaka Magazi a Yesu Khristu ndi kumuyeretsa iye.

<sup>116</sup> Kenako, iye atachita izo, usiku wina iye akudutsa ndipo akumva chinachake. Iye akupita ndi kukamvetsera. Iye akumva za ubatizo wa Mzimu Woyera, kudzazidwa kwa Mzimu. Kenako iye akuyang’ana pa izo, “Oh, mai, kodi izo sizopambana! Koma, akuti, izo zingawononge utumiki wanga ngati ndingalalikire izo. Izo zingapangitse amayi kundithamangitsa kunyumba. Iwo anganditulutse ine mu mpingo wanga ngati ine ndingati ndipite

konse mu izo. Oh, kulibwino ine ndichoke kwa izo. Koma ndiroleni ine ndiyang'ane kupyola izo. Inde, icho ndi Choonadi, Baibulo.”

<sup>117</sup> Chabwino, monga mtumiki wina wotchuka, wodziwika padziko lonse, anapezedwa posachedwapa (ndi mwamuna amene anali ndi ine mu Puerto Rico) pa mawondo ake, akuyankhula mmalirime, mu London, England; mamuna wamphamvu, mmodzi wa avangeri aakulu mu dziko lero. Ndipo mwamuna uyu, mchimwene wake pokhala ndi ine pano, munthu wodzazidwa ndi Mzimu, anathamangira kwa iye ndipo anati, “Oh, m'bale, ndi zimenezotu.”

<sup>118</sup> Iye anati, “Ine ndikudziwa izo. Ine ndikudziwa izo. Koma, taonani, ndirole ine ndikuuze iwe chinachake.”

<sup>119</sup> Iye anati, “Lalikira izo tsopano. Lalikira izo. Ora lake ndi lino. Ndi chikoka chako, iwe ukhoza kugwedeza dziko.”

<sup>120</sup> Iye anati, “Ayi, sindingathe kulalikira izo. Mwaona, a—mpingo ukhoza kundikana ine. Ine sindingalalikire izo. Ine sindingachite zimenezo.” Oh, m'bale!

<sup>121</sup> “Kukhala a-... anayeretsedwapo ndipo anabwera kudzalandira chidziwitso cha Choonadi, kuyang'ana mu Icho, nkuwona kuti Icho ndi cholondola; ndipo nkupotolokako, powona kuti iwo akudzipachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu, ndi kumuchititsa Iye manyazi poyera, kuchita nawo manyazi Uthenga.”

<sup>122</sup> Paulo anati, “Ine sindikuchita nawo manyazi Uthenga wa Yesu Khristu, pakuti Iwo ndi Mphamvu ya Mulungu yaku chipulumutso.” Ndi Mphamvu ya Mulungu ikugwira ntchito pakati pa Mpingo Wake.

<sup>123</sup> Koma iwo anati, “Ine sindinathe kuchita zimenezo.” Munthu uyu anati, “Iwo akhoza kuganiza kuti ndine wa chipentekoste. Iwo angandipange ine...” Iye anati, “Yanga—mbiri yanga ingawonongeke.” Oh, m'bale!

<sup>124</sup> Ine ndiribe mbiri. Ine ndikuganiza za Yake. Mbiri Yake, ndi Iyeyo.

<sup>125</sup> Koma taonani momwe iwo angabwerere moyandikira kwa Iwo, inu mukudziwa, “Ndipo nkuwatenga Magazi a pangano amene iye anayeretsedwa nawo, chinthu chimene chinamuyeretsa iye ndi kumuchotsa iye mu dziko, ndi kuyesera kumuyika iye cha Kuno. Ndipo kenako iye nkuyang'ana pa Iwo, ndipo nkukhala ndi chidziwitso cha Iwo. Nkuchokako kwa Iwo, sipakhalanso nsembe ya tchimo,” linatero Baibulo, “koma kuyembekezera kowopsya kwa chiweruzo ndi mkwiyo wamoto ukuyenera, udzatero, umene udzamuwononge mdaniyo. ‘Pakuti kubwezera ndi kwanga,’ atero Ambuye. Iye amene ananyoza chilamulo cha Mose, anafa wopanda chifundo, pansu pa mboni ziwiri kapena zitatatu. Koposa kotani chilango, ndi

chilango chowawa, ngakhale chiri choyenera, mtumiki amene anapondereza magazi a Yesu Khristu pansu pa mapazi ake, atatha kulandira chidziwitso cha Choonadi, ndi kuchiwerengera Icho ngati chinthu chosayera.” Psyii!

<sup>126</sup> Mukuona pamene ife tiri? Yesu anati, “Samalani.” Mukuona momwe Yudasi anakhalira? Iye anali limodzi ndi iwo. Iye anali Esau, wopangidwa wamkulu kwa m’badwo uno. Iye anali wachinyengo, wotsanzira, anapangidwa kukhala wamkulu kwa m’badwo uno. Apa iye akubwera kwa, kenanso, m’bale wake wa Yesu, m’bale wonyengezera. Koma mu mtima mwake, iye amakhala ndi mpingo wakale wachithupithupi nthawizonse, chifukwa uko ndi kumene iye anamugulitsako Yesu. Iye anamugulitsa Yesu, ukulu wakubadwa wake, mochuluka basi monga momwe Esau anachitira ndi nyansi za mphoza. Iye anagulitsa maukulu akubadwa ake ndi zidutswa za siliva sarte.

<sup>127</sup> Amuna ndi akazi ambiri lero agulitsa ukulu wakubadwa wawo wauzimu chifukwa cha kutchuka kwina, kanthu kena kakang’ono ka dziko kamene inu simumagonjetsa konse; ena aang’ono, akazi, odziphoda ndi kudula tsitsi, kumavala zovala zazifupi; amuna, chifukwa cha nthabwala zazing’ono zonyansa ndi kusuta ndudu, chinachake cha mdziko. “Ngati mukonda dziko kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu,” linatero Baibulo.

<sup>128</sup> Ine sindikufuna kukupwetekani inu, koma ife tafika kumapeto. Ife tikubwera tsopano, tikukwera makwerero mofulumira tsopano.

<sup>129</sup> Mukuona momwe izo zikukhalira? Iwo akuchita zimenezo. Iwo anakonzedweratu. Iwo akhoza kutsanzira ndi kukhala okoma ndi odzichepetsa, apafupi basi, monga Akhristu, apafupi kwambiri mwakuti akanadzanyenga Osankhidwa omwe; koma ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.

<sup>130</sup> Mkazi atavala akabudula, samawoneka nkomwe ngati Mkhristu, kwa ine. Baibulo linati, “Ndi chinthu chauchimo komanso chamanyazi kuti mkazi azimeta tsitsi lake.” Mkazi mmodzi yekha mu Baibulo anapenta nkhope yake, anali Yezebeli.

<sup>131</sup> Nanga bwanji amuna, amuna inu amene mukuyenera kukhala amuna Achikhristu, ndipo mukuwalola akazi anu kuti azichita zimenezo? Pamene, Mulungu adzakufunsani inu kuti mudzayankhe pa izo! Osati mwamuna! Mwathupi! “Oh, ine ndituluka ndiye ndi kukajowina mpingo uwu.” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. “. . . inu muganize za zimenezo.” Ndizo ndendende basi chimene Lemba linati iwo akanadzachita, ndipo ndizo ndendende basi zimene iwo achita. Ndipo ndi zimene iwo ati adzachite, kunyengerera!

<sup>132</sup> Winawake anati, “Billy, ngati iwe susiya zimenezo, uthamangitsa aliyense.”

<sup>133</sup> Pali Chinthu chimodzi chimene sichingapite, Mzimu Woyera, chifukwa Iwo ndi Mawu Ake. Ndipo wokhulupirira weniweni wodziwidwiratu sadzachoka, chifukwa Iwo ndi Chakudya ku moyo wake. Iye amawakonda Iwo. Palibe chimene chingamuchotse iye kwa Iwo. Iye adzachita chirichonse, monga Yakobo, koma iye akufuna ukulu wakubadwa umenewo. Iye adzayima pamenepo. Sindikusamala ngati izo zitengera kutaya bwenzi aliyense yemwe ali naye, ngati izo zitengera ntchito yake, ngati izo zitengera umembala wake wa mpingo, ngati izo zitengera chirichonse. Iye adzagwiritsitsabe kwa izo, chifukwa iye sangapirire izo. Muli chinachake mwa iye, chikumusuntha iye, chakuya chikuyitanira ku Chakuya. Oh, ndi inu apo, chinachake mwa iye!

<sup>134</sup> Taonani, chirichonse chimene inu mukufuna kuchipeza mu Baibulo, ndi kuchitenga icho apa, bwererani ku Genesis ndipo mukawone pamene icho chinachokera, muwone pamene icho chinafikako. Mizimu yonse ndi mayendedwe lero akubwerera ku Genesis. Ndi chimene ife tachita, kuti titsimikizire kwa inu zinthu izi zimene inu mukuziwona, abwenzi. Musaiwale zimenezo. Musalole izo zipite pamwamba pa mutu wanu. Mulole izo zilowerere mwa inu. Ndizo zinthu za Mulungu. Izo zafika kumutu; ndipo Yesu ananeneratu izo kuti zidzafika kumutu kenanso mmasiku otsiriza, ndipo zidzakhala motere: Chisindikizo cha Mulungu, ndi chilemba cha chirombo; mphanvu ziwiri zauzimu zikugwira ntchito pamodzi.

<sup>135</sup> Tsopano, aliyense akudziwa kuti Chisindikizo cha Mulungu ndi ukulu wakubadwa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Aefeso 4:30, amati, “Musawukwiytse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Pamene iwo anabadwa mwatsopano, iwo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ndi Kubadwa kwatsopano, ife tikudziwa zimenezo. Ndinu—ndinu wobadwa mwa Mzimu, ine ndivomereza zimenezo. Koma kufikira inu mutabadwa!

<sup>136</sup> Pali mwana wobadwa mmimba mwa amayi ake, amakhala moyo wantundu wina. Umenewo ndi moyo, ndipo ndi aang’ono. . . makhungu aang’ono mu thupi lake akuzipotokola ndi kumamenya ndi kumalumhalumpha monga *choncho*. Koma iye akabadwa, amakhala a. . . [M’bale Branham akuwomba mmanja kamodzi, akutsanzira kambama—Mkonzi.] monga *choncho*, ndipo kenako iye amalira mokweza, amakhala solo yamoyo.

<sup>137</sup> Ndipo mwana akhoza kupita ku tchalitchi ndi kukati, “Oh, ine ndimakhulupirira mu mpingo. Ine, ine ndipita, ine ndikachita *ichi*. Ndipo ndine wabwino. . . Ine ndikufuna kuchita bwino, ine ndikufuna kuchita bwino.” Koma chimene iye akusowa ndi kumenyedwa kwa Uthenga kuti umuwukitse iye, kuti alilire ku Moyo Wamuyaya; ndipo Mzimu Woyera umafuula mwa iye, ngati Iwo sunafuulepo. Kenako iye ndi cholengedwa

chatsopano, ndi wobadwa mwa Mzimu. Zikatero amayamba kukula, kusuntha, ndipo amakhala ndi umunthu wake mwa Mulungu; mwaona, monga ngati khanda, khanda lachirengedwe, limakhala ndi umunthu wake mdziko.

<sup>138</sup> Ndiye ngati msasa wapadziko lapansi uwu upasuka, ife tiri nawo wina ukuyembekezera, mwaona. Motsimikiza basi monga thupi lachibadwa linkabwerera, pali thupi lauzimu loti lidzambulandire iye pamene adzagwa kuchokera kwa amayi ake. Ndipo pamene iye adzagwa kuchokera kwa amayi, dziko lapansi, limene liri, iye ali mmimba mwake tsopano, akubuula, akulira, (O Mulungu!), akubuula, akuvutika, akukalamba, ndi matenda, ndi chirichonse kumulepheretsa iye, ndipo mzimu mkati mwake ukufunafuna dziko kutsidya kwa mtsinje. Ndipo ukubuula, ukupotokola, ukulumpha, (inde, bwana) chifukwa kuli moyo kumeneko umene umakhala kwanthawizonse. Iye ali mu thupi limene likuyenera kufa. Ndipo nthawiyina, monga momwe mayi anagwetsera mwana wathupi, ndipo thupi lauzimu linamulandira iye; dziko lapansi lidzagwetsa, ndipo thupi lachirengedwe lidzagwetsa, ndi thupi lanyama. . . kapena thupi lakumwamba lidzawakha ilo kumeneko. Ngati msasa uwu wapadziko lapansi upasuka, tiri nawo wina umene ukudikirira. Ndi chifukwa chake inu mumaiwala zinthu za mdziko. Izo nzakufa, kwa inu. Apo pali Mzimu.

Tsopano penyani izo pamene ife tikupitirira tsopano, mizimu iwiriyo.

<sup>139</sup> Mzimu Woyera ndi Kubadwa kwatsopano, ife tikudziwa zimenezo. Ndi kubadwa kachiwiri, mwa Mzimu wa Mulungu. Umo ndi momwe inu mumabadwira, mwa Mzimu. Kubadwa mwa Mzimu, ndiko Kubadwa kwatsopano. Chabwino. Inu mumabadwa mwa Mzimu; ndiye pamene inu mwabadwa mwa Mzimu, mumadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Chabwino.

<sup>140</sup> Ndiye pamene ziwiri izi ziri mdziko lapansi, chachirengedwe ndi chauzimu, nthawizina. . . Ine ndaziwonapo izi. Tsopano potseka, ine ndikufuna kuti ndifike kotseka tsopano, ponena izi kwa maminiti pang'ono. Mu chirengedwe kapena mu uzimu, chimodzicho. . . Tsopano ndikuyembekeza kuti aliyense amvetse ichi. Tsopano mungokhala chete basi ndi molemekeza momwe mungathere.

<sup>141</sup> Tsopano, kodi inu munayamba mwachiwonapo ichi? Inu mmawona mmipingo yathu lero, ngakhale mmagulu amene ife tadzilekanitsa tokha ndi kupanga mabungwe; ndipo taziwona zonsezi. Ndipo inu mwamuwonapo munthu akutenga Lemba linalake, ndipo, m'bale, munthu ameneyo akhoza kutenga Lemba limenelo ndi kulipanga ilo kukhala lamoyo mwatsopano, kulipanga ilo kukhala chimodzimidzi basi chimene chinalonjezedwa apa mu Baibulo. Ndipo munthu wotsatira adzamuwona iye akuchita izo, ndipo iye adzabwera

apo ndi kudzayesera kuti achite izo, ndipo nkulephera. Ine ndikudalira mukuwerenga tsopano. Iye adzalephera. Chifukwa chiyani? Lembalo ndi losadzozedwa kwa iye. Iye akungoyesera kutsanzira. Iye akuyesetsa kuti achite monga chinachake. Iye sanali. . . Chabwino, mwinamwake anatumidwa ndi munthu. Mwinamwake munthu wina anati, “Chabwino, inu mukhoza kuchita chinthu chomwecho.” Mwaona, chimodzimodzi monga momwe Yesu ananenera kuti zikanadzakhala mwanjira iyi. Baibulo limaneneratu izo mmasiku otsiriza, “Monga Ayane ndi Yambre anamutsutsira Mose.”

<sup>142</sup> Pamenepo panaima Mose, ndipo apo panayima Yambre. Ndipo Mose anaponyera pansu ndodo yake, ndipo inasanduka njoka. “Bwanji,” Farao anati, “bwera kuno, Yambre, iwe ukhoza kuchita chinthu chomwecho.” Ndipo iye anatero, mwaona. Koma chinachitika nchiyani? Kenako ndodo ya Mose inadya ndodo yake. Mwaona, izo zinawonetseredwa. Kodi ndodo yake inali kuti?

<sup>143</sup> Monga ngati kuzindikira kwapamwamba. Ziri ngati zina za zamizimu izi. Ziri ngati yina ya mipingo iyi imene iwo amakhulupirira mwachithupithupi, kutali kwambiri. Zinthu za. . . Iwo amati, “Bwanji, izo zinali za tsiku lina.” Iwo onse ali kunja. Koma tawuwonani mzimu uwu mmasiku otsiriza ukupita kukatsanzira Mzimu weniweni. Mukuona? Pamenepo ndi pamene vuto lanu likubwerapo. Ndendende basi monga iwo umene uli weniweni, mwaona; koma iye sanathe kuwupanga iwo kuwonetseredwa, iye sakanakhoza kuwugwira iwo, iye sakanatha kuwupanga iwo kukhalitsa. O Mulungu!

<sup>144</sup> Anthu amabwera ndikuti, “Ine ndiri ndi Mzimu Woyera, nanenso.” Yang’anani momwe iwo amakhali; izo sizimakhala kuchokera ku chitsitsimutso chimodzi kupita ku chimzake, kuchokera ku msonkhano umodzi kupita ku umzake. Izo zimawonetseredwa, iwo alibe Iwo. Ngati munthu abadwa mwa Mzimu wa Mulungu, kapena mkazi, iwo amakhala ndi zipatso za Mzimu. Iwo amayenda mwaumulungu. Iwo amakhala moyo umenewo. Mukuona? Iwo amadzimatula ku zinthu za mdziko. Mulungu amayenda mwa iwo ndipo amadziwonetsera Yekha, ndipo amatsimikizira kuti Iye ndi Mulungu akugwira ntchito mmenemo. Winayo akutsanzira. Mukuona?

<sup>145</sup> Kutsanzira, ndipo ndi zomwe zakhala ziri mpaka mmusi, kutsanzira. Tamuwonani Ishmaeli, ndi Isaki; ndi onse kumatsika, mwaona, kutsanzira. Tamuwonani mneneri Mose, ndipo tayang’anani pa mneneri Balamu. Mukuona? Muone momwe iwo anatsikira! Tamuwonani Yudasi, ndipo tayang’anani pa Yesu.

<sup>146</sup> Ndipo Yesu amaneneratu kuti Mzimu Woyera uwu, mmasiku otsiriza, udzakhala Chisindikizo cha Mulungu. Tsopano, kodi chilemba cha chirombo chidzakhala chiyani? Kudzakhala



kukana Chisindikizo cha Mulungu. Pakuti, onse amene sanakhale ndi Chisindikizo cha Mulungu anali ndi chilemba cha chirombo. Ndipo ngati ziri zilemba ziwiri zauzimu, chimodzi cha izo chidzakhala chilemba choona cha Mulungu, chinacho chidzakhala chinyengo. Kodi inu mukuziwona izo?

<sup>147</sup> Tayang'anani pa chilemba mu Chipangano Chakale. Pamene lipenga linawomba, chisangalalo, zaka zochulukira chomwecho, a—akapolo ankamasulidwa chifukwa lipenga limawomba. Chabwino, aliyense amene ankafuna kukhala mfulu, amakhoza kumapita. Koma ena a iwo, iwo amakonda kukhala akapolo, chotero iwo ankawatengera iwo ku guwa ndi pa nsanamira ya tchalitchi, ndipo ankawaboola khutu lawo ndi chisongole. Ndipo iwo ankayikidwa chizindikiro kwa nthawizonse, iwo nthawizonse ankatumikira mbuye ameneyo.

<sup>148</sup> Ndipo lero mukamva Uthenga wa uthenga pa Choonadi, “Tsopano inu mukhoza kukhala mfulu ngati mukufuna,” Mulungu akuyankhula ndi inu. Koma pamene inu mufika pa mzere wa malire umenewo ndi kuyang'ana kumeneko, ndi kukhala ndi chidziwitso cha Choonadi, ndipo kenako nkuchokako, iye amakubowolani mu khutu ndipo inu nthawizonse mudzakhala wokhulupirira waluntha. Inu mudzakhala wachipembedzo ndi kumapita ku tchalitchi, koma osadzalandira konse Mzimu Woyera. Mwaona, ndiye inu mudzatumikira zimenezo tsiku lanu lonse. Tsopano, chilemba cha chirombo, kapena Chisindikizo cha Mulungu. Ndipo ife tikuyandikira kwambiri.

<sup>149</sup> Tsopano, taonani, Mawu akuyenera kudzozedwa; kuwamva Iwo, kuwazindikira Iwo, nkuchitapo pa Iwo. Anthu ambiri amawamva, koma osawazindikira Iwo.

Mulungu adzati, “Ili ndi ora la inu.”

<sup>150</sup> “Ine sindingakhale woyera wodzigudubuza. Ine—ine sindikufuna chirichonse cha Iwo.” Mwaona, iwo samawazindikira Iwo.

<sup>151</sup> Ife tipita ku misonkhano, Mzimu Woyera wawukulu ukasunthira kumeneko. Ine ndinali nditakhala kumeneko tsiku lina, pamene masomphenya anabwera ndipo ananeneratu ndendende basi chimenecho. Ine ndinati, “Apa pakubwera mnyamata.” “Bwera kuno,” ndinamuuza wotheadizira uyo, “iwe uli ndi vuto la mtima ndipo ukufunafuna a . . .”

“Eya. Ndizo kulondola ndendende.”

<sup>152</sup> “Mukuona mkazi uyo akubwera apoyo?” “Bwera kuno. Iwe uli ndi chotupa pa bere, ndipo icho chiri pa bere la kumanzere, ndipo iwe uli mu chikhalidwe choyipa kwambiri. Ndipo ndiwe wochimwa ndipo su . . .”

“Kulondola ndendende.”

153 Amuna amenewo atakhala pamenepo, akuyang'ana pozungulira, alaliki ndi onse, akuti, “uh-huh!” Kupita ku msonkhano, kukawona Mzimu Woyera ukupita kudutsa mu msonkhano ndi kunena zinsinsi za mitima, zinthu monga choncho. Nkuti, “Zodabwitsa. Ine ndikuganiza. Eya.” Mukuona? Oh, m'bale! Mukuona? Izo—izo—izo ziri mbali inayo, pali chinachake chinachitika. Akazi nkumapitirira kumachitabe, kumachita chinthu chomwecho. Amuna nkumapitirirabe kumabwerera mmbuyo momwe, monga nkumba ku matope ake ndi garu ku masanzi ake, chimodzimodzi basi. Kodi inu simukuona? Tsopano ndikuyankhula kwa a- . . . ndi . . .

154 Mwaona, iwe ukuyenera kuzindikira ndiye, mzanga, chikhalidwe chimene iwe ulimo. Ndi chifukwa chake tepi iyi, ine ndinati, “Kwa mpingo wokha.” Mukuona? “Mpingo wokha.” Ngati mwaitanidwa kuchokera ku kuwala . . . kuchokera ku mdima kupita ku Kuwala, kuchokera ku imfa kupita ku Moyo; kuchokera ku lingaliro lofunda, kumvetsa kwaluntha kwa Khristu, kupita ku chokuchitikira cha kubadwa mwatsopano; ndi kumaona moyo wanu, kuti iwo ukuyika zinthu za mdziko pambali, ndipo inu mukuimira Khristu, mulimonse; ndiye kuti chinachake chinachitika. Mukuona? Muli chinachake mwa inu, chikuchitira njala ndi kusuntha, monga zinakhala ndi Yakobo. Mwaona, inu mukalimbana ndi Ambuye, inu muyenda mosinthika pambuyo pa zimenezo. Chinachake chasinthika mwa inu, inu mwasinthika.

155 Tsopano, izo zatero, izo zisanachitike, izo zikuyenera kuti zidzozedwere kwa inu. Ine sindikusamala, ine ndikhoza kuyima pano ndi kulalikira mpaka ine nditapeza . . . tsitsi limene ndatsala nalo litathothoka, mpaka mapewa anga nkugwera pansu ndipo ine nkukhala wa zaka nainte, ndipo inu mkumamvetsera tsiku lililonse; kufikira Mulungu atafulumizitsa izo kwa inu, inu mukanali mu chochitika chomwecho.

156 Masiku awiri ndakhala ndikuphunzira ndi kupemphera pa izi. Mukuona? Ine ndinati, “Ambuye, kodi ndikanene izo kwa mpingo?”

157 Chinachake chinati, “Kanene izo. Ora layandikira. Kanene izo.” Ine ndikumverera kuti Iye akhala akundichotsapo ine posachedwapa, chotero ine—ine ndikufuna kuti inu mudziwe izo.

158 “Palibe munthu amene angadze kwa Ine,” anatero Yesu, “pokhapokha Atate Anga atamuitana iye poyamba. Oh, ine ndikudziwa inu mumanena kuti muli ndi Mulungu ndi Abrahamu, kwa atate wanu; koma ndikuuzani inu ichi, ndinu . . . atate wanu mdierekezi,” anatero Yesu. Amuna achipembedzo, ansembe, ndi amuna aakulu, “Inu ndinu a mdierekezi, atate wanu.” Mukuona? Zindikirani, zimatso za Mzimu.

159 Tsopano, mwaona, izo zikuyenera kufulumizitsidwa kwa inu.

160 Sindingathe kuganiza kuti Nowa akuti, “Inu mukudziwa chiyani? Izo zikuyenera kuti ikhoza kudzavumba mvula tsiku lina, chotero ine ndingotuluka ndi kukadzimangira chombo. Ngati mvula ingadzavumbe, chabwino, ndidzalowa mu chombocho ndi kumadzapita nthawi yomweyo. Ndipo palibe chimene chidzandivutitsa ine, chifukwa ine ndidzalowa mu chombocho ndi kumadzapita.” Kodi inu mungalingalire? Ayi. Ayi. Izo sizinali zimenezo. Ngati zikanakhala zimenezo. . . Oh, mulole Osankhidwa amve izo tsopano. Ngati izo zikanakhala choncho, wonyoza woyamba amene akanabwerapo, monga Baibulo linati analipo, atamunyoza iye, iye akanaiika nyundo yake pansu, ndi kumachokapo.

161 Monga anthu amachitira lero, izo zimayambira ndi Yesu; ndipo pamene iwo ayang’ana uko ndi kuwona Choonadi, iwo amachokapo kwa Ichu. Iwo sangathe kupirira nacho Ichu.

162 Monga mvangeri wodziwika uja anati, “Ichu—ichu chidzawononga utumiki wanga.” Ine sindisamala za utumiki umene Mzimu Woyera ungawuphwasule. Iwo ukuyenera kung’ambidwa. Tsopano, koma, mwaona, ndi kunyada, anthu ochuluka ambiri, munthu wochuluka. Oh, zindikirani mu ichi tsopano.

163 Nowa anali kunja mmunda, ndipo iye anamva, ndipo iye anazindikira, ndipo anachitapo. Ziribe kanthu ndi onyoza angati anabwera, iye anamanga nthawi yomweyo.

“Nowa, ndiwe woyera wodzigudubuza.”

164 “Sizikundikhudza ine mpang’ono pomwe.” Ankapitirira kumamanga! Iye anali atamva. Iye anali atazindikira kuti iye anali Mulungu, iye anaziweruza izo mwa Malemba, ndipo izo zinani chomwecho. Iye anamangabe chombocho, mulimonsemo.

165 Kodi mungaganizire, inu mungaganizire konse izi, kuti Mose, ali pa ulendo wake ku Igupto, anatuluka tsiku lina ndipo anati kwa Zipporah, mkazi wake, “Zipporah, iwe ukudziwa chiyani? Ndapukuta zina pa galamala yanga. Ine ndawawongola ena a masamu anga aang’ono, ndi ina ya geometry yanga ndi, oh, zinthu zina zambiri, ndi maphunziro anga. Chiyambireni kuweta nkhosa kumbuyo kuno, ine—ine—ine ndakhala ndikupukuta zina mwa izo. Ine ndinalakwitsa uko mu Igupto. Ndikuganiza kuti ndipita kumusi uko ndipo ndikakonza izo. Ndikuganiza kuti ndipita kumusi uko”? Ayi, funde loyamba likanabwera momutsutsa iye, iye akanagwera pomwepo.

166 Kodi iye anachita chiyani? Iye anayiwala zonse zimene iye ankazidziwa za geometry ndi luntha lake. Ndi zimene zinamulowetsa iye mmavuto.

<sup>167</sup> Ndi chimene chawuyika mpingo mu vuto lero, ndi alaliki ophunzira ochuluka opanda kubadwa mwa Mzimu. Amuna ndi akazi okonda kumvetsera zoyankhula zaluntha, mmalo molalikira mphamvu ndi kuwuka kwa Yesu Khristu. Izo ndi zimene zatiyika ife mmavuto lero. Sitikufunanso masukulu apamwamba ndi maphunziro a alaliki. Ife tikusowa amuna oyitanidwa ndi Mulungu amene ali odzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo osati fioloje ina yopangidwa ndi munthu ya chipembedzo china. Ife tikusowa amuna oyitanidwa ndi Mulungu.

<sup>168</sup> Mose ankaweta nkhosa, anakhazikika pansi ndipo anaziyiwala. Iye ankadziwa kuti mzeru zake zinali zitalephera. Iye ankadziwa kuti maphunziro ake anali atamulephera iye. Iye ankaweta nkhosa, koma iye anamva, oh, “Vula nsapato zako, Mose, nthaka yomwe wayimapoyo ndi yoyera.” Iye anamvetsera kwa ilo. Icho chinali chiyani? Liwu limene Mngelo anayankhula linali la Mwamalemba. Iye anamulonjeza Abrahamu, abambo ake, “Ine ndidzawachezera anthuwo atatha kukhala kuno kwa zaka foro handirede, ndipo Ine ndidzawatulutsako iwo ndi nkono wamphamvu.” Iye anazindikira kuti ilo linali Lemba la Mulungu likuwonetseredwa.

<sup>169</sup> Mundirole ndiyimikire kamphindi. Mulole izi zizamirire mkati. Kodi inu mukuona chimene ine ndikunena lero? Mawu a Mulungu akuwonetseredwa pamaso panu pomwe, ndipo inu simukuwazindikira iwo. Taganizani tsofano za Sodomu ndi Gomora; taganizani za lonjezo la Khristu ku masiku otsiriza.

<sup>170</sup> Mose anazindikira izo; zinali Mwamalemba, ilo linali lonjezo. Iye anamva, iye anazindikira. Chinachake chinadzabwera mwa iye, m'bale, iye akanatha kupita ndi kukazichita izo ndiye. Iye anachitapo. Iye amakhoza kupita kumusi ndi kukayimitsa Farao aliyense. Iye amakhoza kukaitanitsa miliri pamene iye wafuna. Iye anakhoza kukatsegula Nyanja Yofiira, chifukwa iye anali atamva, iye anali atazindikira, iye ankachitapo mmalo mwa Mulungu.

“Ine ndidzakhala Mulungu kwa iwe, iwe ukhale mneneri kwa Ine,” Iye anatero.

Ndipo iye anati, “Ine sindingachite izo.”

<sup>171</sup> Iye anati, “Chabwino, ndiye, iwe ukakhale mulungu, ndipo Aroni akakhale mneneri wako. Iwe ukuyenera kumapita, mulimonse.”

<sup>172</sup> Iye sanangoti, “Chabwino, mwinamwake ine ndikuyenera kupita kumusi ndi kukawongola zinthuzo.”

<sup>173</sup> Kodi inu mungalingalire Eliya pa Phiri la Karimeli, akuti, “Inu mukudziwa, dziko ili ndi lochimwa kwambiri, mwinamwake, mwinamwake ine ndikuyenera kupita kunja ndi kukamuza Ahabu kuti iye akuyenera kudzichitira yekha manyazi. Mwinamwake ine ndikuyenera kuti ndipite

pamwamba pa phiri uko ndi kukakhala pansi, ndi kukasala basi motalika kwambiri, mpaka anthu amenewo atadwala kwambiri ndi kutopa ndikundiwona ine pamwamba apo ndikufa ndi njala”? Ayi. Ayi. Izo sizinali zimenezo.

<sup>174</sup> Koma iye anamva, ndipo iye anazindikira, ndipo iye anachitapo. “Ine ndalamulira makhungubwi kuti akakudyetse iwe. Pita kumeneko, ku Keriti.”

<sup>175</sup> Itafika nthawi ya chiwonetsero pakati pa Baala ndi Mulungu, iye anati, “Mupite, mukatenge nsembe zanu, mukachite chirichonse kwa iwo chimene inu mukufuna, ndipo mukaitanire pa mulungu wanuyo.” Pamene iwo anadzicheka okha, ndipo anali ndi mnofu wochuluka, ndipo analumpha mmwamba ndi pansi, anali ndi phokoso lambiri, iye anati, “Fuulani mokweza pang’ono, mwinamwake iye wapita, akupita kwinaakwake. Iye mwina akugona.” Oh, m’bale!

<sup>176</sup> “Chabwino, inu mukudziwa chiyani?” Iye anati, “Ine ndine wokhulupirira mwa Yehova, chotero ine ndikhoza kuchita izi, mulimonse.” Oh, ayi, musati muzitsanzira zimenezo. Ayi. Musati muyesere kukhala Eliya mpaka Mulungu atakuitanani inu kuti mukhale. Inde, bwana. “Ine ndine wantchito wa Yehova.” Pali seveni handirede a iwo kumusi uko, aponso, koma palibe mmodzi wa iwo anayerekeza kuti achite izo.

<sup>177</sup> Kenako pamene iye anayidula ng’ombeyo ndi kuthira madziwo, iye anati, “Ambuye, ine ndachita ichi mwa lamulo Lanu.” Mwaona a . . . Wina aliyensenso akanakhoza kuyesera, zikanakhoza kukhala kulephera kwathunthu.

<sup>178</sup> Zikuyenera kudzozedwera kwa iwe! Mzimu Woyera ukuyenera kuzibweretsa izo ndi kuzipanga izo kuwonetseredwa kwa iwe.

<sup>179</sup> Ndiro limene liri vuto lero. Iwe sungathe kuyimirira, pa guwa, ndi kunena, “Chabwino, Aleluya, Aleluya. Ambuye, ine ndikufuna Mzimu Woyera. Aleluya, Aleluya.” Ayi.

<sup>180</sup> Koma, m’bale, mlongo, pamene Mzimu Woyera wawadzozero Mawu amenewo kwa iwe, iwe uwatenga Iwo usanachokepo pa mpando wakowo. Chinachake mwa iwe chitentha. Mlaliki sasowa kuti achite kukuuzwa iwe kuti uchite *ichi* ndi kuchita *icho*. Masamba akalewo adzangogwa, ndipo masamba atsopano adzatulukirapo. Izo zimadzozedweratu kwa iwe. Iwe sungakwiye ndi mlaliki akamalalikira Choonadi chochokera mu Baibulo. Iwe udzachikonda Icho, udzachifikira Icho. Ndi Chakudya ku solo yako.

<sup>181</sup> Ngakhale Yesu, Iyemwini, Iye anati, “Ine sindichita chimene ndikufuna kuchita, mwa Inemwini. Mwana sangachite kanthu koma chimene Iye awona Atate akuchita.” Mawu . . . Iye anali Emanuele, Iyemwini. Iye anali Mulungu pa dziko lapansi; Yesu anali. Iye anali mnofu umene Mulungu ankakhalamo. Iye anali chihema chimene Mulungu ankakhala pansi pake. Ameni. Koma

mu zonsezo, Mwana wa Mulungu wobadwa mwa namwali, Emanuele mu chidzalo cha Mzimu, Iye anali ndi Mzimu mopanda muyeso. Ndipo, komabe, mu thupi Lake Lomwe, Iye anati, “Ine sindimachita kanthu mpaka Atate atandiwonetsera Ine poyamba.” Kudzozedwera kwa Iye, kuti akachite izo!

<sup>182</sup> Satana anati, “Sandutsani miyala iyi ikhale mkate, ndipo muchite chozizwitsa. Ndiroleni ine ndikuwoneni Inu mukuchita icho.”

<sup>183</sup> Iye anati, “Kwalembedwa, ‘Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha.’” Oh, mai! Koma pamene khamulo linali ndi njala, Iye anatenga mabisiketi faivi ndi tinsomba tiwiri, ndipo anadyetsa faivi sauzande. Oh, Aleluya! Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>184</sup> Musayesere kutsanzira. Ndiro limene liri vuto ndi Pentekoste lero. Ndiro limene liri vuto ndi mpingo lero, pali ambiri akuyesera kutsanzira kuti iwo ali ndi Mzimu Woyera. Pali ochuluka akuyesera kutsanzira machiritso Auzimu. Pali ochuluka kwambiri akuyesera kutsanzira zinthu zosiyanasiyana za Ambuye. Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Zinthu zimenezo zimabwera mwa kusankha, Mulungu akuyitana, iwe umabweretsedwa kuchokera mmimba ya amako ndi zimenezo. “Mphatso ndi mayitanidwe ziribe kulapa.” Oh, mai! Izo ndi zoon. Inu simungathe kudzipanga nokha chinachake chimene inu simuli.

<sup>185</sup> Koma ngati Mulungu akuyitana iwe, ukhale munthu woyamikira kwambiri padziko chifukwa Iye wakuyitana iwe. Ndiye izo zimakhala zenizeni kwa iwe.

<sup>186</sup> Monga ine ndingati ndiyankhule, ngati ine ndikanakhala ndi nthawi, pa agologolo tsiku lina, pafupifupi kunditembenuza ine mozungulira. Ine sindinaziwonopo izo, ndipo sindikanachita izo. Hattie, wakhala kumbuyo uko akundiyang’ana ine. Kodi zimenezo zikanachitika bwanji? Izo sibwenzi zitachita zimenezo, koma izo zinali zodzozedwa, zofulumizitsidwa. Mawu anayankhulidwa ndipo anapangidwa chomwecho. Aleluya!

<sup>187</sup> Paulo, mungamuganizire iye akuti, “Ine ndakhala ndiri pa nyanja iyi kwa masiku fortini ndi mausiku, ndipo opanda nyenyezi kapena mwezi, kapena dzuwa kapena kalikonse. Ndikuganiza ndingopita kumtunda uko ndi kukawauza iwo, ‘Limbani mtima, chifukwa Mulungu atisamalira ife, mulimonse’?” Oh, Mulungu samagwira ntchito monga choncho. Mulungu samachita zimenezo.

<sup>188</sup> Chikhulupiriro chanu chiri bwino, m’bale. Chikhulupiriro chanu ndi chopambana. Koma kufikira chinthucho chidzozedwere kwa inu!

<sup>189</sup> Oh, apa pali nyali yofiira ili apoyo, ndipo ngati ine ndikuona...ndikuti, “Chabwino, ine ndiyika phazi langa powonjezerera motopa. Ndiri ndi galimoto. Ine ndikhoza

kudutsa pa getsi limenelo apo, ndikuthamanga mailosi handiredi ndi twente pa ora.” Izo nzoona. “Ndikukhoza kumva mphamvu pansu pa phazi langa.” Koma inu kulibwino mudikirire mpaka chizindikiro chakuti “pitani”. Aleluya!

<sup>190</sup> Kodi inu mukumvetsa chimene ndikutanthauza? [Osonkhana Akuyankha, “Ameni.”—Mkonzi]. Pamene chizindikiro cha “pitani” chabwerapo, zonse zabwino. Pamene chinthucho chadzozedwera kwa iwe, ndipo Mulungu wachipangitsa icho kudziwika monga Iye anachitira kumbuyo uko, zonse ziri bwino. Koma kufikira Iye atachita izo, ife tiri ndi gulu la a Yudasi akutsanzira, akuyenda limodzi mofanana, kumati, “Chabwino, ndine chimodzimidzi monga iwo ali. Ndine Mkhristu, nanenso.”

<sup>191</sup> Oh, kodi inu simukukumbukira? Ana a Skeva—Skeva anatuluka ndipo anati, “Ife tikukulamulira iwe, tikukulamulira iwe mu Dzina la Yesu amene Paulo amamulalikira. Tuluka!”

Iye anati, “Paulo ndikumudziwa, ndipo Yesu ndikumudziwa, koma inu ndi ndani?”

<sup>192</sup> Ora likudza pamene chabwino ndi choyipa chidzawonetseredwa. Zikuwonetseredwa mwa Akhristu lero. Izo zikuwonekera mmipingo lero. Izo zikuwonekera mwa anthu lero. Ine ndikukusungani inu motalikitisa; ndikufuna izi zifike kwa inu.

<sup>193</sup> Paulo sananene kuti, “Ndikukhulupirira ndingopita ndi kukati, ‘Chabwino, khalani olimba mtima.’” Ayi.

<sup>194</sup> Kodi iye anachita chiyani? Iye anamumva Mngelo. Iye anadziwa kuti uyo anali Mngelo yemweyo amene nthawizonse ankayankhula kwa iye. Iye anazindikira, kenako iye anachitapo. Anapita uko ndipo anati, “Khalani olimba mtima. Pakuti Mngelo wa Ambuye, Amene ine ndiri mtumiki Wake, anaima pafupi nane usiku watha, kundiwonetsa ine masomphenya kuti sipadzakhala kalikonse kotayika, pa sitima iyi. Khalani olimba mtima. Pitani mukadye chakudya chanu chamadzulo tsopano. Zonse ziri bwino.” Ameni. Pamene izo zadzozedwera kwa iwe, pamene Mulungu azikonza izo!

<sup>195</sup> Ine ndiri ndi ndemanga apa penapake, ine ndinali nditayilemba. Apa iyo ili pomwe apa. Uh-huh. Ife tiri kumapeto a zinthu zonsezo. Ndiroleni ine ndingobweretsa izi monga chonchi tsopano, potseka. Ine ndikuyembekezera kuti Mulungu waulula chinachake kwa inu. Penyani. Chirichonse chiri kumapeto. Winawake anafunsa usiku wina, ine ndikukhulupirira anali M'bale Fred Sothmann, ife timafunsa za mapeto a nthawi ayandikira motani.

<sup>196</sup> M'bale Demos Shakarian anali atawona masomphenya amenewo akuwonetseredwa kwambiri, ndipo anakwaniritsidwa masiku faivi atadutsa, mwangwiro, izo zinangokhala ngati

zamugwetsa iye kuchoka mu nsapato zake. Iye anandiyimbira ine. Iye anati, “Joseph ali bwanji?”

Ine ndinati, “Ali bwino.”

Anati, “Kodi iye amawona masomphenya?”

<sup>197</sup> Ine ndinati, “Eya. Iye anandiuza ine za David, mwana wamwamuna wa M’bale Wood, pamene iye anagwa pa njinga yamoto, masiku atatu kapena foro izo zisanachitike, ndendende basi.”

Iye anati, “Inu mukudziwa, zinthu zimenezo zimatsatira mabanja.”

<sup>198</sup> Ine ndinati, “Chirungamo kapena choyipa, zimatero, chimodzi cha izo. Zimatsatira mabanja.”

<sup>199</sup> Ndipo ife timayankhula pang’ono, ndipo iwo, Fred anati kwa ine, “Kodi izi zikuchokera kuti, M’bale Branham?”

<sup>200</sup> Ine ndinati, “Taona, Fred, tiye tizitenge mwachirengedwe. Mulungu amagwira ntchito mu chirengedwe Chake. Taona, tayang’ana chimene chinachitika. Dzuwa limatulukira Kumawa. Chimenecho ndi chitukuko chakale kwambiri chimene ife tiri nacho, ndi China.” Ife tonse tikudziwa zimenezo.

<sup>201</sup> Chitukuko chakale kwambiri chimene tiri nacho ndi China. Chabwino. Ndipo chitukuko chasunthira cha kumadzulo nthawi yonse. Ndipo tsopano kodi inu mungapite kuti ngati inu mutachoka ku Gombe la Kumadzulo, kupita molunjika kuwoloka? Mupita ku China. Ndendende. Ife tiri kumapeto. Baibulo linati, mneneri anati, “Lidzakhhalapo tsiku limene sikudzakhala usiku kapena usana, pamene dzuwa lidzadzadutsa, koma mu nthawi ya kumadzulo,” basi izo zisanathere apa, “kenanso padzakhala Kuwala, chimodzimodzi.” Yesu anati, “Padzakhala mvula yoyamba ndi ya masika. Ndipo mvula ya masika idzabweretsa mvula yoyamba ndi ya masika, mu nyengo yomweyo.” Ife tiri kumapeto a nthawi.

<sup>202</sup> Yang’anani apa, ndiroleni ine ndikuwonetseni inu. Ndale ziri kumapeto. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndiwonetseni ine chinachake lero. . .

Fuko lino ndi loyipitsitsa kwambiri mdziko, la chivundi, lopanda umulungu. Ndi ndani amene anawerenga pepala la Courier Journal usiku wina, mu Louisville, pamene akazi onse awa, akutenga, fuko lirilonse, mkazi wokongola kwambiri mu fukoli, ndi kuwayimitsa iwo kuti akhale Abiti Universe? Aliyense anatero kupatula Russia. Ndipo anatumiza kwa Khrushchev ndipo anamfunsa iye, “Chifukwa chiyani?” Iye anati, “Russia samavula akazi ake, kuti aziyenda pamaso pa amuna.” Mtundu wachikunja, wopanda umulungu kubweretsa chitonzo pa ife amene timadzitcha tokha Akhristu, anati, “Russia samavula akazi ake, kuti aziyenda kunja monga choncho. Ndipo simudzawona akabudula kapena zinthu zotero



ku Russia.” Zimenezo ndi kupanda umulungu. Ndipo ife amene timadzitcha tokha “Akhristu”!

<sup>203</sup> Nzosadabwitsa Baibulo linati, “Gome lirilonse ladzaza masanzi. Ndipo ndi ndani amene ine ndingamuphunzitse Chiphunzitso, ndi amene waletsedwa kuyamwa? Koma lamulo lidzikhala pa lamulo, ndi mzere pa mzere. Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena Ine ndidzayankhula kwa anthu awa. Ndipo uwu ndiwo Mpumulo. Pa zonsezi, iwo sanamve.” Ife tiri ndi kuganiza kwathu kwa luntha. Oh, momwe zikanakhaira zabwino kukhala tsiku lonse pa Izo.

<sup>204</sup> Ndale, zavunditsidwa! A Democrat, a Republican, ndi onse, atsikira pansi. Icho ndi chiyani? Ndi gulu la kumezanitsa. Munthu aliyense amene amagwira ntchito mmenemo, amene sanabadwe mwatsopano, ndi wa mdierেকেzi. Mdierেকেzi anati, “Ufumu uliwonse padziko ndi wanga,” ndipo Yesu sanatsutsane naye konse. Dziko lapansi likulamulidwa ndi mdierেকেzi. Ndipo munthu aliyense amene amagwirira ntchito m'boma, ngati iye sali Mkhristu, iye ndi wa mdierেকেzi ndipo akumugwirira ntchito mdierেকেzi. Mafuko onsewa adzagwera kwa Yesu Khristu pamene Iye adzabwera, padzakhala Zakachikwi.

<sup>205</sup> Tayang'anani apa lero, chimene iwo akuchita tsopano. Kundiwozoza ine za kuwonongera ndalama kunja uko kwa Akhristu, ndi kufuna kundipatsa ine zaka twente mu ndende ya boma, chifukwa chowononga ndalama kuti ndiziyendetsa kasunthidwe ka chipembedzo. Ndipo akachasu ndi mowa ndi ndudu zimawononga mateni a mamillioni a madola pa chaka, kuti avunditse fukoli. Ndipo ine ndikuyesetsa kuti ndilalikire chirungamo, nditayima pa khomo la Yesu Khristu, ndi kunditumiza ine ku ndende chifukwa cha izo. Ndi kutenga zinthu ngati zimenezo za oyipa, otsikitsitsa, anzeru, zaluntha, ndipo nkuwalola iwo awononge izo chifukwa cha maprogramu a pa televizioni amene avunditsa dzikoli, atumiza akazi kwa agalu. Limodzi la matemberero aakulu kwambiri amene fuko linayamba lakhalapo nalo, ndipo iwo amapitirira nazo izo. Iwo akunditumiza ine ku ndende chifukwa cholalikira Uthenga, kutenga madola angapo kuchokera kuno kuti—kuti ndikalalikire Uthenga, amene anthu amandipatsa ine kuti ndizilalikirira Uthenga. Ine si wolemera ndipo sindingathe kulemba izo. Komabe iwo akufuna kunditumiza ine ku ndende, kukandisungako ine zaka ziwiri, ndipo ndiri ndi mlandu ukubwera posachedwapa. Oh, zotsika pansi bwanji, zonyansa bwanji! Mulungu, atichitire chifundo.

<sup>206</sup> Ine ndinena chinthu chimodzi ichi, mwinamwake umo ndi momwe Mulungu wazikonzera Iye asanatumize bomba la atomiki. Inu mukuyenera kuchita chinachake cholakwika, inu mukudziwa. Inu mukuyenera kukhudza wodzozedwa Wake nthawi imodzi, kwa Lemba lomweli ili, kuwopa kuti... “Musakhudze Wosankhidwa Wanga.” Uko nkulondola. Chotero

ngati izo zikuyenera kutengera izo kuti zibweretse chiweruzo, monga izo zinachitira mmasiku a Daniele kapena kwinakwake, ziloleni izo zibwere. Ine ndine wantchito Wanu, Ambuye. Uko nkulondola. Oh, inde.

<sup>207</sup> Ndale, zatsika pans! Fuko, lavunda! Chabwino, taonani chiyani! Iwo ayika asirikali atavala akabudula tsopano. Oh, mai! Ndale, nkondo! Ndale ziri kumapeto. Olamulira mwankhanza akulakwitsa. Ndale ndi zolakwika. Chifukwa chiyani iwo sanakhale ndi mfumu yaumulungu monga Mulungu anawapatsa iwo, Davide? Mbuye wamkulu waku England anati, pamene iyi—pamene demokalase iyi inakhazikitsidwa, anati, “Izo zonse ziri bwino tsopano, koma idzafika nthawi,” iye anati, “Iyo siyidzakhala kanthu. Zonsezo zidzakhala kuyenda pa nyanja wopanda nangula.” Ndipo iye akulondola. Anati, “Andale amaima pa mabokosi a sopo pakona iliyonse, mitundu yonse ya zinthu zokhotakhota zimene zikuwononga boma.” Ndipo munthuyo ankulondola. Ndendende zimene zikuchitika.

<sup>208</sup> Munthu mmodzi akhoza kupita kunja kuno, ndi kupita kudutsa apa ndi kukaledzera, ndi kukakhadzula chirichonse chimene iye akufuna; ndi kupita kumusi uko, iye amamudziwa aliyense, chotero palibe chimene chimanenedwa. Mulole munthu wosauka, kapena winawake wosadziwika, ayesere kuchita zimenezo, ndipo iwo amatumizidwa kundende. Chiphuphu, zotsikitsitsa kwambiri, nyansi, forte peresenti ya iwo ogonana amuna okhaokha. Taganizani za zimenezo, Sodomu ndi Gomora kenanso! Ndi limenelo gululo, likuyenera kukhala lachipembedzo.

<sup>209</sup> Ine—ine ndikudabwa chimene chidzachitike motsatira, pamene Purezidenti wotsatira adzabwerepo? Mulungu anatipatsa ife munthu mmodzi wabwino waumulungu, Dwight Eisenhower wokalamba. Ndipo tsopano ine ndi-... Penyani chinthu chotsatira chimene chikubwerapo. Ndipo ife tikhoza kudzakhala ndi khoswe nthawi yotsatira, ndithudi mokwanira. Koma akubwera, “Faro amene samamudziwa Yosefe.” Kumbukirani zimenezo. Ine ndifika kwa izo mu mphindi chabe. Ndale zavunda. Ife tikudziwa zimenezo.

<sup>210</sup> Nkhondo ili kumapeto ake. Oh, iwo ankaponyana miyala nthawi yina pa wina ndi mzake, ankamenyana wina ndi mzake pamutu ndi nkhwangwa zamiyala, kenako nkumaponyerana mivi ndi uta. Kenako iwo anatenga mfuti, kenako mfuti za makina, kenako ma eyite eyiti ku Germany, ndi mifuti yaikulu kwambiri ndi ife. Kenako iwo anaponyera mabomba a mmanja ndi mpweya wapoyizoni. Koma iwo ali ndi bomba la haidrojeni tsopano. Nkhondo ili kumapeto. Fuko lirilonse liri nazo, ndiye inu muchita chiyani tsopano? Ngakhale fuko laling’ono lero, kungokolekera chowombera, ndizo zonse zimene iwo akuyenera kuchita, ndipo ilo lonse lidzapita mmwamba. Nkhondo ili

kumapeto. Huh! Ameni. Nkhondo ili kumapeto. Ndale ziri kumapeto.

<sup>211</sup> Maphunziro ali kumapeto. Kulowerera kwa ana kuli kumapeto. Ana, palibe chiyembekezo kwa ana, iwo apenga. Inu simungakhale ndi maphunziro. Inu simungapite kumusi kuno ku sukulu ndi kukhala, kupeza mwana wa maphunziro. Iye ndi— iye amakhala mwana wofutukuka pawiri wa gahena pamene iye akutuluka kuposa momwe amalowera. Mulole mphunzitsi anene chinachake pa izo, iye aphedwa. Iwo apanga Klux yaing’ono ndi kupita kunja uko ndi kumuombera mphunzitsiyo, kumutulutsa iye ndi kumumanga iye. Ife tinataya aphunzitsi thu sauzande. Oh, dikirani miniti, ine ndikukhulupirira anali aphunzitsi twente sauzande, chaka chathachi. Ine sindikuwaimba mlandu iwo. Ine sindikanafuna kuchita izo, ngakhale. Tsopano iwo ali ndi zikwangwani nthawi zonse, “Perekani maphunziro aku koleji kwa ana awa.” Iwo akuwafuna iwo, koma mdierekezi anawagwira iwo. Mdierekezi anawagwira iwo. Ndipo izo sizachizolowezi basi kutuluka ndi kukhala wankhanga ndi— ndi—ndikuchotsa chipata ndi kuchipachika mumtengo pa usiku wa Halloween, kapena kuchita zoipa pang’ono monga momwe ana ankachitira, kapena kutenga ngolo ya mlimi ndi kuyiyika iyo pa msewu, osati monga choncho; koma iwo ndi amisala. Iwo amachita zinthu zimene ziri zamisala; kukuombelani, kukuphani, kukuphani, kukuikirani poyizoni, chirichonse. Umenewo ndi m’badwo wotsatira.

<sup>212</sup> Kubereka ana kuli kumapeto, ukazi, umayi. Bwanji, kulera kukuchitidwa paliponse, ndipo agalu aang’ono atenga malo.

<sup>213</sup> Makhaliidwe, palibenso makhaliidwe kwa izo. Akazi, akuvala moipa; kubwera kudutsa mu televizioni, mitundu yonse ya zotsanzira za anthu oyipa aku Hollywood, mitundu yonse ya zinthu, mafashoni. Zonse ziri kumapeto!

<sup>214</sup> Maphunziro ali kumapeto. Ndale ziri kumapeto. Nkhondo ili kumapeto. Chitukuko chiri kumapeto. Zinthu zonsezo ziri kumapeto. Mai, tingachite chiyani ndiye? Chotsatira ndi chiyani? Ife tiri kumapeto kwa zinthu zonse.

<sup>215</sup> Tsopano moyo wa mpingo uli kumapeto, mpingo wamba, mpingo. Tsopano, izi zikhoza kumamatira pang’ono pokha, koma mpingo wachithupi, mpingo wa Esau, iwo wafika pa mapeto ake. Kodi iwo ukuchita chiyani? Ukupita mu chitaganya cha mipingo, umene pamapeto pake udzalumikizana ndi Chiroma, kuti amenyane ndi Chikatolika...kapena ndi Chikatolika kumenyana ndi chikominisi. Papa Yohane akuyitanitsa mipingo yonse kuti ibwerere, ndipo iyo yatero. Ndipo iwo adzadzilumikizitsa okha limodzi, ndendende basi chimene PAKUTI ATERO AMBUYE.

<sup>216</sup> Inu mukuti, “Dikirani miniti, M’bale Branham. Inu mukuchoka pa mzere.” Ngati ine ndikutero, Mulungu analemba

Baibulo Lake atachoka pa mzere. Iwe ukuyenera kukhala Mikaya, pa nkhani iyi.

217 Morris Cerullo anandiuza ine usiku wina, anati, “Ali kuti wotsutsakhristu, M’bale Branham? Myuda ndi wotsutsakhristu.”

Ine ndinati, “Morris! Ndipo iwe, Myuda?”

Iye anati, “Iwo ndi odana ndi Mulungu kwambiri amene alipo.”

218 Ine ndinati, “Morris, usatero! Ndiuze ine mu Lemba pamene wotsutsakhristu anachokerapo ku Yerusalemu. Wotsutsakhristu amachokera ku Roma, osati kuchokera ku Palestina.”

Iye anati, “Chabwino, onani, ine...Iwo ndi odana ndi Mulungu.”

219 “Inde, kodi Mulungu sananene kuti Iye anachititsa khungu maso awo kuti tikhale ndi tsiku lopenya? Koma tsiku lathu litha posachedwapa.”

220 Iye anati, “Oh, M’bale Branham, ine sindinaganizepo za izo.” Mwaona, ndi inu apo.

221 Mwaona, ife tiri kumapeto. Dziko lachithupithupi, mpingo wachithupithupi uli pa izo, kumapeto. Yang’anani momwe zikuyendera mu chitaganya cha mipingo. United Brethren analowa mu icho. Achipentekoste ali mu icho. Ena onse a iwo amadzipanga okha bungwe. Kukuonani inu uko, Akanani awo, njira yonse mpaka kupyola mu mizimu ya Esau iyo, achipembedzo kwambiri, ndipo anadzipangitsa okha chitaganya ndi dziko; osakhala ndi kumvetsa kwauzimu, osatha kugonjetsa, osati osankhidwa a Mulungu, kuti ayitanidwe atuluke ndi kupatulidwa.

222 Oh, ngati ine ndikanakhoza kuchidziwitsa icho, pamene ine ndikanakhoza kokha kuchikankhira icho pansi mwanjira yina! Iwo sakuziwona izo. Iwo ali ndi maso ndipo sakutha kuwona, makutu ndipo sangamve. Oh, chifukwa chiyani ife tiri opanda nzeru mu Mzimu? Tsopano, mvetserani kwa ichi. Chirichonse chiri kumapeto.

223 Ndipo Mpingo wauzimu uli pa mapeto Ake. Iwo ukubwera ku mapeto. O Mulungu! Tayang’anani kumbuyo uko pamene Iwo unayamba ndi Luther, anagwedezera pansi, auzimuwo. Kenako ndi Wesley, kubwera ku kuyeretsedwa. Kenako ndi Pentekoste, Mzimu Woyera. Ndipo tsopano ku mapeto a nthawi, Mzimu wa Khristu chomwecho mu Mpingo, Iwo ukuchita ntchito zomwezo zimene Iye ankazichita, kubwerera ku Mutu Wake kenanso; kukonzekera kuti Mpingo ndi Khristu agwirizane, ndi Kudza kwa Ambuye Yesu, ndi chiukitsiro cha akufa. Ife tiri kumapeto a nthawi. Yesu anatero, “Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwecho izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Kodi inu mukuzimvetsa izo?

224 Yang'anani pa mpingo wachithupithupi. Yang'anani kumene iwo akupita, kutali ndi kutali.

225 Yang'anani pa Mpingo wodzazidwa ndi Mzimu, ukuchotsa zopusa Zake zonse, ukubwera mu Mzimu, (mwa awochepa, ndithudi), ukubwera mu Mzimu, koma ukusunthira mmwamba kupita mmalo oterowo mpaka Iwo utafika kumeneko kumene Mzimu Woyera ungamasunthire kudutsa mwa Iwo, ukugwira ntchito mwanjira Yake, wokonzekera kuti ulandire Ambuye wake, wokonzeka kuti ulandire Ambuye wake.

226 Ndipo ena onse a iwo anapanga bungwe, akubwerera ku dziko, kugawikana, kubwerera mu chitaganya, kusunthira mmwamba mu mutu umodzi waukulu wa chitaganya pansi pa Chikatolika. "Ndipo panali fano linapangidwa la chirombo." *Fano*, "chinachake chonga icho." Chitaganya cha mpingo chopangidwa ndi Chikatolika, awiri amenewo pamodzi, kumagwira ntchito limodzi. "Ndi ndani angathe kuchita nkondo ndi chirombo kapena fano lake?" Ndithudi ayi. Momwe ife tingakhoze kudutsira mu izo kwa maora!

227 Tsopano ndiroleni ine ndinene ichi kwa inu, ndipo kenako ikhala nthawi yoti titseke. Ndi ine...Ndinakuuzani kuti zikhala motalika. Ine—ine ndimangomverera wosokonezeka kwambiri. Pamene Mulungu ananena zinthu izi, anati, "Awuze iwo. Ukaziyankhule izo. Usakakhalenso chete mopitirira. Kawawonetse Iwo kwa iwo. Ngati iwo sakawalandira Iwo, ndiye magari sali mwanja mwako." Ora lafika. Nthawi, zonse zikupita mmwamba.

228 Dziko liri pamapeto ake. Ilo silingapirirenso. Nkhondo ziri pamapeto ake. Simungathe kukhala ndi nkondo yina. Ngati muli ndi nkondo, izo sizitero; basi woyambayo amene ati adzakhethemule kowombererako, ndi zimenezo. Ndale, zaola ndipo zavunda.

229 Dziko la mpingo ndi Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achipentekoste. "Ndi nkumba ku matope ake, agalu kumasanzi ake." Uko nkulondola, aliyense wa iwo! Mulungu akuitana, kuchoka mu chivundi chimenecho, Mpingo umene wasankhidwa. Ndizo ndendende. Esau, iwo anati, "Ndife mpingo!" Sindikukayika zimenezo. Yakobo anali atate wa Esau, nayenso, ndiko kulondola, chotero, koma—koma...Ine ndikutanthauza, Isaki anali atate a Esau, ndipo Yakobo anali mchimwene wake, ndi iye. Koma wina anali ndi kulemekeza ukulu; winayo ankadana nawo. Winayo anamva, anazindikira, ndipo anachitapo. Winayo anati, "Oh, bola ngati ine ndimapita ku tchalitchi ndipo ndimachita chimene chiri cholondola, kodi izo zimapanga kusiyana kotani?" Ndi zimenezotu. Tsopano mu...

230 Ine ndikunena ichi ndiye, potseka, ndemanga ina yowonjezera iyi. Mpingo weniweni uli ndi zambiri zoti

uzikhalira moyo tsopano. Oh, iyo ikuyenera kukhala nthawi yachisangalalo chotero kwa Mpingo weniweni, kwa Mpingo woona, kwa Mpingo wosankhidwa, pamene inu mukudziwa mu mtima mwanu kuti mwadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo; pamene inu mudziyang'ana nokha ndi kuwona, kuyang'ana moyo wanu ndi kuwona kuti zinthu zonse zapa dziko zapita, kuti mwakhala cholengedwa chatsopano. Mvetserani tsopano, potseka, mwatcheru. Inu mukudziwa kuti mwadutsa, moyo wanu umatsimikizira izo, “Ndi zipatso zawo mudzawadziwa iwo.” Cholinga chanu chonse ndi Khristu. Inu mukuyembekezera Iye kuti abwere miniti iliyonse. Inu mukumayenda mu Mzimu. Inu mukumukonda Iye. Inu mukumuona Iye akugwira ntchito kudzera mwa inu. Palibe chimene inu mukukhumba kuti muchite, koma Iye amachita icho, Iyemwini. Oh, ndi nthawi yotani!

<sup>231</sup> Zimandikumbutsa ine za wojambula amene anapita ku Roma, kukaphunzira kukhala wojambula, mnyamata wamng'ono. Iwo anamuzindikira iye. Iye anali wosiyana kwambiri ndi anyamata ndi atsikana onse aku America, ndipo zinthu zimene zinkachitika kumeneko kuti akakhale ojambula, ndi ochokera ku dziko lonse. Mnyamata mmodzi ameneyu anali wapadera. Iye anali munthu wabwino, ndipo iwo anazindikira. Iwo ankakhala ndi maphwando aakulu kwambiri, ndi kufika kumeneko ndi, momwe iwo amachitira mu Roma, amangoledzera momwe iwo angathere.

<sup>232</sup> Ine ndinapitako kumeneko, inemwini, ndipo ndinawaona iwo. Akutuluka pa msewu, amuna ndi akazi, ndi kumapitirira. Ngakhale mu mapaki, amakhala ndi zogonana mu paki, kunja komwe poyera, osalabadira; England, nayenso, ena onse a iwo. Mukuona? Izo sizoyipitsitsa kuposa kuno. Basi chinthu chomwecho apa, pafupifupi moyipa kwambiri; basi, kungobisa izo mochulukira pang'ono apa, nkhani za apolisi ndi chinthu. Tsopano, koma zoipa basi!

<sup>233</sup> Chabwino, mnyamata wamng'ono mmodzi uyu, iye anadzapatula yekha kwa izo zonse. Pamene iwo apita ku maphwando awo, iye ankawasiya iwo azipita, koma iye ankaphunzira kukhala wojambula. Chotero, tsiku lina wosamalira wakale, amene anali Mkristu amene anali pafupi ndi—ndi miziyamu, yazojambulajambula, iye anati—iye anati, “Tiye tiyende pang'ono, mwana. Tiye tiyende, ndikufuna ndiyankhule nawe kwa kanthawi.”

Iye anati, “Chabwino.”

<sup>234</sup> Chotero iwo anapita, akuyenda kukwera phiri, ndipo awiri onse a iwo manja awo ali kumbuyo kwawo, anayenda kukwera phiri. Dzuwa linkalowa. Ndipo chotero mwamuna wokalambayo anati kwa wojambula wamng'onoyo, iye anati, “Mwana, ndiwe waku America.”

Iye anati, “Ndinedi.”

<sup>235</sup> Iye anati, “Iwe wabwera kuno kuti udzapeze maphunziro ako mu zojambula. Ine ndikuganiza kuti ukufuna kupanga ntchito ya moyo wako kukhala wojambula.”

Iye anati, “Ine ndikukonzekera kuchita izo, bwana.”

Anati, “Ine ndikuzindikira kuti ndiwe Mkhristu.”

Iye anati, “Ndine Mkhristu.”

<sup>236</sup> Iye anati, “Chabwino, pali chinthu chimodzi chimene ine ndikufuna ndikufunse iwe. Ine ndawafunsa enawa. Iwo akuti iwo ndi Akhristu, nawonso.” Iye anati, “Nchiyani chimakupanga iwe kukhala wosiyana kwambiri? Nchiyani chimakupanga iwe wosiyana ndi anyamata ena onse ochokera ku America, ndi atsikana awa ochokera ku America? Nchiyani chimakupangitsa iwe kusiyana kwambiri, ndipo komabe inu nonse mumati ndinu ‘Mkhristu’?”

Iye anati, “Bwana, mukuona momwe dzuwa ilo likulowera?”

Iye anati, “Ine ndikutero.”

<sup>237</sup> Iye anati, “Kutsidya kwa nyanja, mu chigawo china ku New England, mu mzinda wina wa chigawo chimenecho, ndipo mu nyumba inayake mu mzinda umenewo, muli mtsikana winawake amene ine ndinamulonjeza kuti ndidzakhala moona kwa iye.” Iye anati, “Ndizo zonse zimene ziri mmaganizo mwanga, kuti ndipeze maphunziro anga a zojambula ndipo ndidzabwerere kwa mtsikana ameneyo amene akukhala moona kwa ine.” Iye anati, “Umo ndi momwe ndimakhallira chimene ndimachita.”

<sup>238</sup> Oh, m’bale, mlongo, inu mukhoza kudabwa chifukwa chimene ife sitisamala chimene iwo amatitcha ife. Ine sindisamala chimene iwo akunena.

<sup>239</sup> Ine ndinali nditaima ndi Fred tsiku lina, uko mu San Juan, Puerto Rico, ndinkayang’ana kutsidya kwa nyanja, ndipo ndinazindikira, thanthwe la coral lija, theka la mailo kunja, mafunde aakulu awo akuswa. Iye anati... Atsekwe akuyenda mmunda, zina zotero. Ine ndinati... Iye anati, “M’bale Branham, izi ziri ngati Kumwamba.”

<sup>240</sup> Ine ndinati, “Koma nyanja idzakhala chete kumeneko, m’bale.” Ine ndinati, “Kutsidya la nyanja kotaliko, kuli malo ena otchedwa Kumwamba, kuli Mmodzi wotchedwa Yesu, Kumwamba uku, amene tsiku lina Iye anachotsa machimo anga onse. Ndipo ine ndinamulonjeza Iye kuti ine ndidzakhala moona kwa Iye, ine ndidzachita zinthu zimene Iye ankafuna kuti ine ndichite. Ndicho chifukwa ine sindikuchita manyazi ndi Uthenga Wake, Iwo ndi Mphamvu ya Mulungu yaku chipulumutso.” Icho ndi chimene chimampangitsa Mkhristu kukhala wosiyana. Iye ndi wosiyana chifukwa ali ndi Chinachake choti adzichikhalira moyo mosiyana.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe.

<sup>241</sup> Mzanga wokhumudwa, mmawa uno, iwe uli ndi china chosiyana choti uchikhalire moyo, chinachake choti chikutulutse iwe mu dziko, chinachake chimene chimatanthauza zochuluka kwa iwe kuposa dziko lonse, ndi kumukhalira moyo Khristu? Ngati iwe ulibe icho, bwanji iwe sukulandira Icho tsopano. Osangopita ku tchalitchi ndi kukati, “Ine ndikufuna kukhala munthu wabwino.” Usachite zimenezo. Iwe ukufuna kukhala Mkhristu. Iwe, ngati pali chinachake nthawizonse chakhala mu mtima mwako, chikukuuza iwe, “Iwe sukulondola, koma ndikufuna kuti ukhale olondola.” Iwe nthawizonse umalalaka kukhala chinachake chimene iwe suli tsopano, kodi iwe sukudziwa kuti ndi Mulungu akukuitana iwe? Usatembenezireko nsana wako. “Pakuti ngati inu munawunikiridwapo kamodzi ndikukhala ndi mwayi, ndipo munawukana nthawi yanu yomaliza, pamenepo sipanatsalenso nsembe yochotsera tchimo.” Musakhale mbali ya Esau.

<sup>242</sup> Bwerani ndi Yakobo, mosasamala za a . . . mosasamala za chimene chingachitike. Ngati izo zitengera nyumba yanu, ngati izo zitengera ntchito yanu, ngati izo zitengera mwamuna wanu, izo zitengera mkazi wanu, ngati izo zitengera ana anu, ngati izo zitengera chirichonse, pezani ukulu! Icho ndi chimene chimafunika. Ndipo ngati inu mukumverera motero za izo, mmawa uno, ndipo mukufuna kukhala ndi ukulu uwu! Ine sindingapereke Iwo kwa inu. Mulungu akhoza, ndipo Iye ndi Amene akuyankhula kwa inu. Kodi mungakweze dzanja lanu, kunena, “Ndipemphererani ine, M’bale Branham. Ukulu uwo, ine ndikuufuna.” Mulungu akudalitseni inu, kulikonse mozungulira. “Ukulu umenewo, ine ndikuufuna.”

<sup>243</sup> Atate athu a Kumwamba, ndikukuthokozani Inu, Mulungu Wolemekezeka ndi Woyera, chifukwa cha ubwino Wanu wonse ndi zifundo zanu kwa ana aamuna ndi aakazi a anthu. Ndipo ife tikuzindikira kuti ife tiri ku mapeto a nthawi, palibe chimene chingapite motalikirapo. Ife tikungodikira mu nthawi yobwereka; monga zinaliri mmasiku a Nowa, kuleza mtima kwa Mulungu, pamene chingalawa chinkakonzedwa, pamene miyoyo eyiti yokha inapulumutsidwa. Inu munati, “Chomwecho kudzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu. kuleza mtima kwa Mulungu, osafuna kuti aliyense awonongeke, koma kuti onse afike ku kulapa.”

<sup>244</sup> Ndipo lero mu nyumba ino, muli amuna ndi akazi akweza manja awo, anyamata ndi atsikana, aang’ono ndi aakulu, akweza manja awo, ndipo akuti, “Pali Chinachake chikundikoka.” O Mulungu, mulole iwo asachikane Icho. Mulole iwo agulitse maphunziro awo, mulole iwo agulitse chirichonse chimene iwo ali nacho. Monga munthu amene anapeza ngale yaikulu; iyo inali yodziwika, ngale yayikulu, iyo inali ngale yapamwamba, ndipo iye anagulitsa aang’ono ake onse, kuti iye agule ngale yodziwika



iyi, yapamwamba. Mulole iwo agulitse chirichonse chimene iwo ali nacho cha mdziko, mmawa uno, kutchuka kwawo konse kwa mdziko.

<sup>245</sup> Akazi awa akhala apa, Ambuye, ambiri a iwo amene amvapo Uthenga ukulalikidwa nthawi zambiri, ndipo akungopitirirabe kulowa mu dziko, ndi mafashoni ngati dziko ndi kumavala monga dziko, ndi kumapita ku maphwando ndi zinthu zimene dziko, kumachita nawo zinthu za chidziko ndi kumachita ngati dziko, ndi kugwiritsa ntchito zinthu za mdziko. O Mulungu, mulole iwo achite manyazi, mmawa uno. Ngati muli chiyembekezo chirichonse mwa iwo nkomwe, Ambuye, tembenuzani icho lero. Lolani ili likhale oralo.

<sup>246</sup> Ndipo amuna awa pano, Ambuye, O Mulungu, achitireni chifundo iwo. Ambiri a iwo akuyendabe mu zinthu za mdziko, akukhumbabe ndi kusangalala nazo zinthu za mdziko, tchimo, kusuta, kumwa, zakumwa zoredzeretsa, mowa pang'ono pambali, kapena—kapena chinachake chonga icho, kapena angakhumbire, ndi kupachika tizithunzi, akazi aang'ono ovala monyansa. Ndi matupi awo amene iwo amawayang'ana pamsewu, ndipo iwo amatsala pang'ono kuwagunda anthu kuti aziyang'ana iwo, nkumadzitcha okha Akhristu.

Ndipo nkumadziwa kuti mawonekedwe awo a thupi la mkazi ameneyo, mwina mu maora twente foro, adzakhala akuvunda uko ymanda, njenjete ndi mphutsi zokwawa ziri mu mitsempha iyo youbika ndi kupangidwa ya thupi lake; ndi solo yake uko mu gehena ya mdierekezi, chifukwa cha momwe iye ankakhalira. Ndipo, komabe, iye amayika mmwamba milomo yake yaing'ono, yopakidwa utoto, ndi kunyogodola ndi kukusekani inu.

<sup>247</sup> Mulungu, achitireni chifundo anthu amenewo. O Ambuye, musawalole kuti atayike. Chonde achitireni chifundo ndi kutumiza chifundo. Apatseni aliyense wa iwo, Ambuye. Inu ndinu Mmodzi yekhayo amene mungapereke mdalitso uwu. Ndipo ngati Inu mwawaitanira iwo ku Moyo Wamuyaya, mulole mitima yawo itseguke; ndipo iwo ayike chirichonse pambali mmawa uno, ndipo kenako iwo alandira icho. Perekani izi, Atate.

<sup>248</sup> Ndipo tsopano mulole Mzimu Woyera ubwere mu msonkhano uwu, kwa odwala ndi osautsika, ndipo mulole anthu awone kuti Uthenga uwu umene walalikidwa mmawa uno, kuti Kudza ndi chirichonse chiri pa mapeto, ndipo ngakhale Yesu akugwira ntchito mu Mpingo Wake. Mulole izo zichitike pakali pano, Ambuye, kuti Inu mukhoze kuwatengera anthu awa mmanja Mwanu. Ndipo pamene iwo awona Mzimu Woyera ukugwira ntchito, ukusuntha pakati pa anthu, mulole izo zitsimikiziridwe, Uthenga umene ine ndaulalikira, kuti ife tiri pa nthawi ya kumapeto. Ndipo mulole iwo amve. Iwo amva, ndipo mulole iwo azindikire kuti Yesu yemweyo, momwe Iye anachitira izo mu tsiku Lake, Iye ali pano akuzichita izo

kupyolera mu Mpingo Wake mu tsiku lotsiriza. Ndipo kenako mulole iwo achite, popereka miyoyo yawo ndi matupi, ndi miyoyo ndi mizimu, kwa Iye. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, Ambuye, mu Dzina la Yesu.

<sup>249</sup> Tsopano, mu chimango momwe muli anthu, Ine ndinamutumiza Billy mmawa uno kuti adzapereke makadi apemphero. Iye. . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

<sup>250</sup> Kodi inu mukudwala, osowa? Ngati Mulungu ati awulule kwa ine, monga Iye anachitira ndi mkazi pa chitsime, ndi kundiuza ine chimene vuto lako liri, kapena chinachake chokhudza inu, chimene inu mukudziwa kuti ine sindikuchidziwa, kodi icho chingakupangitseni inu kukhala ndi chikhulupiriro kuti mukhulupirire Mulungu? Kodi icho chingakupangitseni inu nonse kukhala ndi chikhulupiriro? Kodi iyi ndi nthawi yathu yoyamba kukumana? [Mlongo akuti, “Ayi”—Mkonzi]. O, unandionapo ine, koma ndine mlendo kwa iwe. Ndi kulondola uko? Chabwino, Ambuye Mulungu apereke chopempha chako.

<sup>251</sup> Tsopano, kodi ndi zenizeni, kapena ayi? O, mai! Itanani chipembedzo chanu chaluntha. “Baalimu,” anati, “iye ali kuti?” Eliya pa Phiri la Karimeli, anati, “Baalimu ali kuti? Kuti? Mudzutseni iye.” Simukuyenera kumudzutsa Yesu. Iye amakhala maso nthawi zonse. Iye ndi wopezeka nthawizonse, wamoyo nthawizonse, wokhoza nthawizonse; yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Amen. Mulungu akadali Mulungu.

<sup>252</sup> Iwe ukukhulupirira kuti vuto la mtima wako likusiya iwe ndipo iwe ukhala bwino? Iwe si wochokera kuno. Iwe ubwerere ku Lexington ndipo ukawauze anthu zinthu zazikulu zimene Ambuye wakuchitira iwe. Mukuona?

<sup>253</sup> Izo zimapita pamwamba pa mitu ya anthu, amene samamvetsa izo konse. Mpingo wamoyo ukhoza kuzigwira izo, mwamsanga, ndi kudziwa kuti Kukhalapo kwa Mzimu Woyera kuli pano.

<sup>254</sup> Winawake kumbuyo kuno anakweza dzanja lake. Kodi unali iwe, dona? Iwe ukukhulupirira Mulungu akhoza kundiuza ine vuto lako? Zakale. . .

<sup>255</sup> M’bale kunjwa uko pa mapeto, ine ndikukhulupirira iye ananena, kanthawi kapitako, izo. Iwe ukukhulupirira, m’bale? [M’baleyo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Iwe ukutero? Ndiye vuto la pakhungu ilo likusiya iwe, iwe ukhala bwino. Kodi iwe ukukhulupirira izo? Inu mukuvomereza izo ngati kuchiritsidwa? Kwezani mmwamba dzanja lanu, inu mukutero. Mukuona? Uh-huh. Chabwino. Iye ndi mlendo kwa ine. Iwe ukudziwa zimenezo, Pat.

<sup>256</sup> Dona akuyang’ana pamenepo, akupemphera, anandiyang’ana ine, anati iye ndi mlendo. Iwe ukukhulupirira kuti kuthamanga kwa magazi kukusiya iwe? Uko nkulondola, si

choncho? Kweza mmwamba dzanja lako ngati iko ndi kulondola. Chabwino, ukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>257</sup> Nanga bwanji ena a inu amene mumandidziwa ine? Inu muli ndi chinachake pa mtima wanu. Kwezani dzanja lanu. Ambiri a inu! Ine sindingathe; Izo zikuyenera kubwera basi. Inu mukudziwa, ndi chikhulupiriro chanu.

<sup>258</sup> Georgie Bruce, ine ndikumuona iye atakhala pamenepo. Iwe nthawizonse umayesera kumupezera winawake chinachake, Georgie. Iwe unachiritsidwa, ku khansa. Palibe funso mmalingaliro ako. Tsiku limene iwe unabwera ku kachisi uyu ndi kutuluka pakomo paja, Mzimu Woyera unadza pa ine, ndipo unakuuza iwe apo pomwe kachitidwe kena kamene palibe aliyense mdziko amadziwa koma iwe ndi Mulungu ndi munthu wina. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Uko nkulondola. Iwe ukundikhulupirira ine, sichoncho iwe, Georgie? Iwe uli ndi chinachake pa mtima wako, Georgie. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine chimene chiri mu mtima mwako?

Kodi izo zingakupangitseni inu nonse, anthu amene mukundidziwa ine, kukhulupirira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

<sup>259</sup> Ndimamudziwa Georgie, koma iye akuganiza za chinachake. Iye ali ndi anthu awiri, amene ali kutali ndi kuno, iye akuwapempherera. Onse awiri amakhala ku Corydon. Uko nkulondola. Ndipo iye ali ndi munthu apa, mwamuna amene iye akumupempherera, amene ali kunja kuno mu chipatala. Ndipo iwe ukupemphera, osati kwambiri ku machiritso ake, koma chipulumutso cha moyo wake. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndiko nkulondola. Uko nkulondola, George? Uko nkulondola ndendende.

<sup>260</sup> Winawake kumbuyo uko anakweza mmwamba dzanja lawo, kumbuyo uko kumbuyo, kumbuyo muno. Iwe, nanga bwanji iwe? Kodi ungakweze dzanja lako, ndiwe mlendo kwa ine? Mwamuna uyu wakhala apa akundiyang’ana ine, ine sindikukudziwa iwe. Kodi iwe ukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu, wantchito wa Mulungu? Iwe ukukhulupirira Mzimu Woyera, chimene ine ndanena ndi Choonadi? Iwe ukukhulupirira Izo? [M’baleyo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Ngati iwe ukhulupirira, iwe wa- . . . ndicho chinthu chokhacho chimene iwe uli nacho, chifukwa iwe ukuvutika ndi khansa. Uko nkulondola. Iwe siwochokera mumzinda uno. Ndiwe wochokera ku New Albany. Ndiko kulondola. Ndipo iwe uli ndi khansa. Ngati iwe ukhulupirire ndi mtima wako wonse, iwe ukhala bwino. Kodi iwe uvomereza izo? Kweza dzanja lako. Wodalitsika akhale Ambuye.

261 Ine ndikukhulupirira, mkazi uyo kunjwa uko ali ndi chipewa chowoneka choyera pamutu pake, dona wachikuda, anakweza dzanja lake. Sindinakhalepo ndi munthu wachikuda. Iwe ukukhulupirira, dona? Chabwino, bwana, khulupirirani ndi mtima wanu wonse. Inu muli ndi vuto la mtima, vuto la mmimba, zosokonekera. Winawake wakubweretsani inu kuno mmawa uno. PAKUTI ATERO AMBUYE. Uko nkulondola, sichoncho, dona? Ngati ndiko kulondola, kupiza mpango umenewo umene iwe uli nawo mdzanja lako, kuti anthu awone. Ine sindinamuwonopo mkaziyo mmoyo wanga.

262 Kodi unakweza dzanja lako? Kodi ndine mlendo kwa iwe? Ndipo iwe ndi mlendo kwa ine. Iwe ukukhulupirira kuti Mulungu amandidziwa ine, kapena Mulungu amakudziwa iwe? Iwe ukukhulupirira kuti Iye akhoza kundiuza ine chimene chiri mu mtima mwako? Iwe ukumupempherera winawake. Ndi abambo ako, ali ndi vuto la mtima. Uko nkulondola. Ndipo iwe ukufunafuna ubatizo wa Mzimu Woyera. PAKUTI ATERO AMBUYE.

Ngati iwe ungakhulupirire!

263 Nanga bwanji dona wamng'onoyo atakweza dzanja lake mmwamba monga *chonchi*, iwe ukukhulupirira? Vuto lako ndi zidzolo pa dzanja lako. Koma ukupempherera mdzukulu. Uko nkulondola. Mwanayo sali bwinobwino. Izo nzoona. Sichoncho, dona? Iwe ukhulupirire ndi mtima wako wonse, chifukwa cha izo.

Pamene ine ndinati, “mwana.” Dikirani miniti. O, ndi iwe apo. Mwana wako anachita ngozi ya galimoto; analumala. Ine sindikukudziwa iwe, dona, koma izo nzoona. Ngati ndiko kulondola, kweza dzanja lako.

264 Tsopano, Ndani ali pano? Kodi ndi ndani? Si ine. Ine ndingachite bwanji zimenezo? Musakhale adzansi mu Mzimu, zinthu Zauzimu. Ndi Mulungu pano! Mzimu Woyera umene iwe ukuufuna, kodi iwe ukuukhulupirira Iwo tsopano? Kodi iwe ukuukhulupirira Iwo tsopano? Chabwino, ndiye landira Iwo tsopano. Tsopano ndi nthawi yoti ulandire Iwo. Khulupirira ndi mtima wako wonse.

265 Inu amene mukudwala kapena muli osowa. Ine sindingathe kuchiritsa. Palibe munthu angathe kuchiritsa. Ine sindingathe kupereka Mzimu Woyera. Koma Mmodzi amene angathe kuchiritsa ndi kupereka Mzimu Woyera, Iye ali pano. Iye ndi Mmodzi Amene amachita izo.

266 Tsopano weramitsani mitu yanu. Inu mukhulupirire tsopano, pamene ine ndikukupemphererani inu ndi mipango iyi.

267 Atate athu Akumwamba, monga momwe ine ndikudziwira, ine ndinadutsa mwa aliyense amene anali mlendo, monga momwe ndinadzimvera ndekha ndikufowoka ndi kuzitaya; ndinamverera kutsogozedwa kuti iyi ndi nthawi imene mwina

Osankhidwa ayiwona. Mulole aliyense wa iwo, Ambuye, amene anayitanidwa ndi kuloledwa kuti ayitanidwe mwa Mzimu Wanu; chinachake, chikhulupiriro chawo, iwo anali ndi chikhulupiriro chochuluka (ena a iwo) kuposa momwe iwo ankaganizira kuti iwo anali nacho. Iwo amangoyambira mmitima yawo.

<sup>268</sup> Ndipo mkaziyo anakhudza chovala Chake nthawi yina pamene Iye ankadutsa, ndipo Iye anatembenuka ndikuti, “Ndani wandigwira Ine?”

Ndipo iwo anati, “Chabwino, aliyense wakugwirani Inu.”

<sup>269</sup> Iye anati, “Koma Ine ndimaona kuti ndinafooka.” Ndipo Iye anamupeza mkazi wamng’onyo ndipo anamuuza iye kuti anali ndi vuto la magazi, ndipo chikhulupiriro chake chinali chitamuchiritsa iye.

<sup>270</sup> Ndipo Baibulo linanena, kuti, “Iye akadali Wansembe wa Mkulu, lero, amene angakhudzidwe ndi kumverera kwa zofooka zathu.” Malemba anati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ndipo ngati Iye ali yemweyo, ndi Wansembe Wamkulu yemweyo, Iye adzachita chimodzimidzi ndi kuchita chimodzimidzi.

<sup>271</sup> Ndipo mulole anthu awone kuti Mpingo wodzazidwa ndi Mzimu ukubwera pamutu. Khristu akukonzekera kubwera ndi kudzatenga Mpingo Wake. Zizindikiro Zake zazikulu zotsiriza, monga izo zinali mmasiku a Sodomu; Amene anayankhula, anamudziwa Sarah, ndipo ankadziwa kuti iye anali ndi mkazi wotchedwa Sarah, anadziwa iye mu hema anaseka; Iye anati, “Icho chidzakhala chizindikiro. Pamene inu muwona izo, kumbukirani, m’badwo umenewo sudzatha mpaka zonse zitakwaniritsidwa.” Ndi izi apa. Ife tiri kumapeto.

<sup>272</sup> Perekani, Ambuye, kuti munthu wodwala aliyense muno adziwe kuti Yesu Khristu wamoyo ali pano. Mulole mipango iyi ikhale yodalitsika kwa thupi lirilonse lodwala limene iyo ipiteko. Ine ndikumudzudzula mdierekezi, chifukwa cha anthu. Ine ndikumuponya iye, mwa Mzimu wa Mulungu, mwa chikhulupiriro, ine ndikutaya mthunzi uliwonse wa kukaikira. Mulole munthu aliyense pano, amene anadzozedwera ku Moyo Wamuyaya, alandire Iwo ora lino. Mulole zamatsenga zirizonse, kuzimitsa kwakung’ono kulikonse, kanthu kakang’ono kalikonse ka mdziko, kulemera pang’ono kulikonse, monga Baibulo linanena, “Tiyeni tisiye pambali cholemetsa chirichonse, ndipo tchimo limene limatizinga ife mophweka; kuti tikhoze kuthamanga, ndi chipiriro, mpikisano umene wayikidwa patsogolo pathu; kuyang’ana” (ku chiyani? ku mpingo? ku bungwe?) “kwa Woyambitsa ndi Wotsirizitsa wa chikhulupiriro chathu,” amene ali pano tsopano, “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.” Kuyang’ana kwa Iye Amene. . . Ife sitikuyenera kutenga mawu amene ife tikudziwa kuti ndi owona, komabe Mawu amenewo apangidwa kukhala enieni kwa

ife mmawa uno. Yesu yemweyo amene anafa, si wakufa, Iye anaukanso, ndipo patadutsa zaka thu sauzande Iye akubweretsa Mpingo Wake pamutu. Mzimu wa Yudasi ukugwira ntchito pakati pawo. Koma mulole iwo ayike pambali chopunthwitsa chirichonse ndi chirichonse, ora lino, ndi kumulandira Iye.


<sup>273</sup> Mulole iwo amve, za chimene iwo ali nacho, kupyolera mu ulaliki. Mulole iwo azindikire tsopano kuti Mawu omwewo amene iwo anawamva awonetseredwa, ndipo iwo awazindikira Iwo, kuti Iwo ndi Khristu. Ndipo mulole tsopano iwo achitepo, achitepo pa Iwo: awalandire Iwo, ndi kuyimirira pa mapazi awo, apereke umboni; ndi kulowa mu Ufumu wa Mulungu, podzazidwa ndi Mzimu Woyera.

<sup>274</sup> Mulole odwala achiritsidwe. Mulole osautsika achiritsidwe. Mulole chokhumba cha mtima uliwonse chikonzedwe. Perekani izi, Mulungu Wamphamvuzonse.

<sup>275</sup> Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, mitima yanu yotseguka, ingodzipatsani nokha nyengo ya pemphero; basi tisanachite, ine ndikuganiza, utumiki wa ubatizo ukubwera, basi izi zisanachitike. Pakhala msonkhano wina usikuuno.

<sup>276</sup> Tsopano, kumbukirani, musalole mwayi uwu udutse. Ine ndakhala pano tsopano kwa maora awiri ndi theka, kapena kupitirira, kuyesera kungotenga nthawi yanga, ndi kubweretsamo Uthenga, ndi kuuyala Iwo mkati mwangwiro basi. Ndiye ife timabwera mpaka kumapeto. Ndipo mawu omwewo: kumva, kuzindikira, kuchita. Musalole izo zidutse pamutu panu. Inu mwamva Izo. Kodi inu mukuzindikira kuti Kukhalapo Kwake kuli pano? Kodi inu mukudziwa kuti Ndi Iye amene akukuitanani inu? Ndiye chitanipo pa Izo. Mulungu akhale nanu. Mukhale ndi nyengo ya pemphero.

<sup>277</sup> M'bale Neville, inu bwerani, pang'ono pokha, mu pemphero, ngati inu mungabwere kuno.

Ingomukwezani iye mmwamba. 

60-0221 Kumva, Kuzindikira, Nkuchitapo Pa Mawu A Mulungu  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)